# Buku la Mphunzitsi

Nthawiyabaibulo
Kalasi 0, Yoyamba ndi Yachiwiri

Maphunziro B1 - B6

www.besweb.com

## Bible Educational Services

Registered Charity UK (No 1186004)

**Cholinga cha Utumiki**
Kukonzera ena maphunziro a Baibulo kuti apereke choonadi cha Yesu ku m'bado otsatira pa dziko lonse lapansi.

**Masomphenya a Utumiki**
Kupereka ku m'bado wotsatira maphunziro okwanira, m'chiyankhulo chawo powalembera ndi kuwathandiza komanso kuthandiza anzathu ena onse odzipereka pa dziko lonse.

## ZOYENERA KUDZIWA

**Zomwe a Bible Educational Services amachita**
A Bible Educational Services (BES UK) amasindikiza maphunziro a "Nthawiyabaibulo", "Moyo Watsopano" ndi "Okolola" a m'Chingerezi komanso amathandiza a Postal Bible Schools ndi mabungwe ena amene amagwiritsa ntchito maphunziro a BES ku UK ndi ku mayiko a kutsidya la nyanja pokawachezera, kugwira nawo ntchito limodzi, kuwalangiza ndi kuwaphunzitsa. BES imagwiranso ntchito pamodzi ndi magulu ena amene akugwira ntchito yomasulira maphunzirowa m'ziyankhulo zawo, pomasulira, kusindikiza ndi kupereka maphunziro kwa anthu ena. Maphunzirowa amaperekedwa mwaulere kwa ophunzira onse.

Maphunziro a Nthawiyabaibulo anayamba kugwiritsidwa ntchito ku Kumpoto kwa Ireland zake 60 zapitazo. A Bible Educational Services ndi amene ali ndi udindo woyang'anira ntchito yosindikiza maphunzirowa m'Chingerezi ndi m'ziyankhulo zina zonse. Maphunziro a Nthawiyabaibulo amasindikizidwa mu A4 ndipo amathandiza ophunzira m'madera ena kuti masabata anayi aliwonse azitha kutumiza mayankho ku Postal Bible School Centre kuti akachonge. Posachedwapa, tikuyamika a bungwe la Every Home Crusade (Bungwe la Chitsistimutso) ku Belfast, anayamba kusindikiza maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi amene amatchedwa A5. Amenewa amagwiritsidwa ntchito m'matchalichi ndi m'sukulu makamaka ku mayiko akunja kuti akhale osavuta chifukwa kumeneko njira zotumizira ndi zovuta kwambiri.

Maphunziro a BES ndi apadera kwambiri chifukwa amatha kugwiritsidwa ntchito m'nyumba kapena pa gulu (tchalichi kapena sukulu), potsatira ndondomeko imene imalola ophunzira kuphunzira kwa zaka makumi awiri. Gulu lililonse lili ndi maphunziro asanu molingana ndi zaka zawo, Amene sanayambe sukulu (Kalasi 0), zaka 5-7 (Kalasi Yoyamba), zaka 8-10 (Kalasi Yachiwiri), zaka 11-13 (Kalasi Yachitatu), zaka 14-16 (Kalasi Yachinayi). Pali ndondomeko ya kaphunzitsidwe ya zaka zitatu ya gulu lililonse molingana ndi zaka zawo. (Onani peji 4.) Magulu angathe kusintha molingana ndi kuthekera kwawo. A Bibletime Resource amapereka mpata kwa ana kuphunzira Mawu a Mulungu ndi kutha kuzindikira kufunika kwa Uthenga Wabwino pa miyoyo.

Maphunziro akupezeka m'Chingerezi pa BES website – www.besweb.com kapena kuchokera kwa Mlembi Wamkulu. Amapezekanso pa website ya ziyankhulo zina. BES ali ndi zomwe analemba zothandiza amene akufuna kugwira nawo ntchitoyi, ndipo zimenezi zilinso pa website yawo.

## Keyala

**International and Northern Ireland Secretary (stockist of all English lessons)**
Mr S Balmer, BES Office (UK), 37a Belmore Street, Enniskillen, Northern Ireland. BT74 6AA
Phone: 00 44 286 632 2462
Email: sam@besweb.com

**UK Secretary – Editorial feedback**
Mr Stephen Gillham
Email: stephen.gillham@besweb.com

**Web address:** www.besweb.com
**Email address:** info@besweb.com

## BUKU LA MPHUNZITSI

Poyamba, maphunziro awa anakonzedwa ndi cholinga choti akhale otumizira anthu, koma lero maphunzirowa akugwiritsidwa ntchito kwambiri pamene njira zotumizira ndi zosadalirika. M'madera ena monga ku mipingo ya ku Afrika, India ndi mayiko ena kulibe njira zotumizira zodalirika. Chifukwa cha ichi, Buku la Mphunzitsi linakonzedwa kuti lithandize amene sangathe kulandira pa positi. Buku la Mphunzitsi m'buku lino ndi la Kalasi 0, Yoyamba ndi Yachiwiri.

Buku la Mphunzitsi lililonse lili ndi ndime zonse zimene zili m'maphunziro a Nthawiyabaibulo. Maphunziro a Nthawiyabaibulo ndi Buku la Mphunzitsi zinakonzedwa kuti zigwire ntchito sabata lililonse. Maphunziro a mwezi wa Epulo amafotokoza za Paska ndipo a mwezi wa Disembala za Khirisimasi.

Madera ena amagwiritsa ntchito maphunziro a pa mwezi otchedwa A4, amene ali ndi maphunziro anayi ndipo ena amagwiritsa ntchito maphunziro otchedwa A5 amene ali ndi maphunziro 24. Mphunzitsi kapena mtsogoleri akuyenera kupereka maphunziro a A4, ndipo sabata lililonse azilemba mayankho a phunzirolo m'tchalichi, ku sukulu kapena ku nyumba ndi kupereka mayankhowo sabata lotsatiralo. Kumapeto kwa mwezi, mphunzitsi kapena mtsogoleri adzilandira maphunzirowo ndi kukachonga, akatsiriza abwere nawo ndi kupereka kwa ophunzirawo.

Ngati ophunzira akugwiritsa ntchito buku, mphunzitsi atenge bukulo kumapeto kwa phunziro lililonse ndi kukachonga. Koma tikudziwa kuti madera ena izi ndi zosatheka. Ngati akuphunzira m'kalasi, ophunzira asinthane mabuku awo ndipo mphunzitsi kapena mtsogoleri awathandize kupeza mayankho ndipo ophunzirawo achongelane maphunziro awo. Kumapeto kwa bukuli kuli malo oyika marikisi amene wophunzira wapeza mwezi uliwonse ndiponso malo a ndemanga ya mtsogoleri ya momwe wophunzirayo akuchitira m'kalasi. Palinso satifiketi yomwe wophunzira ayenera kulandira yoonetsa marikisi ake a maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi.

Timakondwera pamene anthu akutifotokozera zomwe akukumana nazo pogwiritsa ntchito Buku la Mphunzitsi ndi mabuku a Nthawiyabaibulo ndipo tumizani ndemangazo kwa stephen.gillham@besweb.com.

## KUKONZEKERA KWA APHUNZITSI

Buku la Mphunzitsi si lotsekeka kuti mphunzitsi sangathenso kuyikapo zinthu zina zomwe akuziona kuti ndi zothandiza pophunzitsa. Nawa malangizo othandiza pogwiritsa ntchito Nthawiyabaibulo.

- **Kudziwa bwino nkhani** - Aphunzitsi akuyenera kudziwa bwino nkhani ya m'Baibulo komanso phunziro la Nthawiyabaibulo lomwe akugwiritsa ntchito. Nkhani ndi yakuti, mphunzitsi awerenge phunzirolo nthawi yophunzitsa isanakwane. Iye amvetse bwino ndondomeko ya phunziro lililonse kuti akonzekere bwino kuphunzitsako.
- **Kumvetsa phunziro lokaphunzitsa** - Poyamba pa ndondomeko ya phunziro lililonse pali mawu akuti, "Ife tikuphunzira kuti" motsatidwa ndi zolinga ziwiri zophunzirira zomwe mwina ana angamvetse ngati mphunzitsi atafotokoza, kenaka pali gawo lotsiriza phunziro la Nthawiyabaibulo. Cholinga chophunzirira ndi kufuna kudziwa nkhaniyo, pamene chachiwiri ndi cholimbikitsa ophunzira kuti aganizire zomwe aphunzirazo ndi kuzigwiritsa ntchito pa moyo wawo. Zolinga zimenezi zikugwirizana kwambiri ndi fundo/choonadi cha m'phunzirolo ndipo aphunzitsi akuyenera kugwiritsa ntchito zimenezi kuti adziwe momwe aphunzitsira ndi zomwe ana aphunzira.
- **Mawu oyamba** - Maphunziro onse akuyamba ndi mawu akuti, "kumene kuli ana" ali ndi zomwe akukumana nazo. Pali njira zambiri zomwe tapereka zothandiza ana kutenga mbali pa zokambirana nthawi ya maphunzirowo.
- **Kuphunzitsa** - Fundo zazikulu za phunziro tapereka. Tikuyembekezera kuti aphunzitsi sadzikhalanso akumaziwerenga pamene akuphunzitsa koma kuti akhala atadziwa bwino nkhani yonse ndipo adzitha kufotokoza nkhaniyo mochititsa chidwi. Mphunzitsi ayesetse kuti ana amvetse mitu ya maphunzirowo kuchokera pa nkhani yomwe akuphunzira ndiponso awathandize kumvetsetsa zoyenera kuchita kuchokera mu nkhaniyo. Pamene m'poyenera tayesetsa kufotokozera bwino monga nkhani chabe. Mawu amenewa tawalemba motere: ***ITALICS***.
- **Kuphunzira** - Nkhani iliyonse ili ndi Vesi Yoloweza. Malo ena muli Mavesi Oloweza awiri; taonjezera vesi ina yomwe tikuona kuti itha kukhala yothandiza kuti ana aphunzire mosavuta. Tikukhulupirira kuti ana adzaphunzira Mavesi Oloweza ndipo aziwakumbukira kotero kuti adzadziwa mavesi ambiri.

- **Kutsiriza** - Kwa amene akuphunzira m'kalasi, mphunzitsi ayenera kudziwa ngati ophunzira angathe kutsiriza ntchito yawo ndiponso za thandizo lomwe likufunika kuchokera kwa mphunzitsiyo. Kwa ophunzira ena padzafunika kuti mphunzitsi aziwerenga nkhaniyo, ophunzirawo n'kumatsatira kapena kumvera. Koma enanso adzatha kuwerenga okha nkhaniyo. M'njira zonse ziwiri, ndi kofunika kuwauza malangizo okhudzana ndi mafunso. Ngati Nthawiyabaibulo sikuchitikira m'kalasi, n'kofunika kuti aphunzitsi azipezeka kuti azithandiza kuyankha mafunso osati aziyankha ngati a m'kalasi wamba. Ophunzira ayenera kumasangalala, kulimbikitsidwa ndi kuyamikiridwa pamene kuphunzira.
- **Kukumbutsana** - Zomwe zingatheke chitani, khalani ndi nthawi ya mafunso, ya masewero ndi zina zambiri. Izi zidzathandiza kuphunzira ndi kukumbukira pamtima nkhaniyo.
- **Kuonetsa** - Nthawi zina, zinthu zoti muonetse zidzakhala zovuta kuzipeza koma ngati n'kotheka yesetsani kupeza zithunzi kapena zida zina zothandiza kuti ophunzira amvetse nkhaniyo. Zinthu zimene ophunzira akuziona zimathandiza kwambiri pofotokoza nkhani. Pamene n'zotheka, pezani zithunzi kuchokera ku www.freebibleimages.org (FBI) zomwe mungathe kulandira. Kumapeto kwa Buku la Mphunzitsi kuli zina zoonjezera momwe akufotokoza kwina kumene mungapeze zithunzi za nkhani za m'Baibulo mwaulere.
- Ngati mungapeze fotokope mutha kukulitsa zithunzizo, kukhala za kalala ndi kuzigwiritsa ntchito pophunzitsa.

## Nthawi ya Phunziro

- **Machitidwe.** M'buku la Mphunzitsi muli machitidwe a phunziro lililonse, koma mphunzitsi ali ndi ufulu nthawi ndi nthawi kusintha machitidwe ake.

1. Mawu Oyamba ndi kufotokoza nkhani - mphindi 15
2. Kuphunzitsa Vesi Yoloweza – mphindi 5 mpaka 10
3. Kutsiriza kulemba - mphindi 20
4. Mafunso ndi zochitika zina mpindi 5 mpaka 10.

Kumbukirani mawu ofunika awa:

"Ndiuzeni ndipo ndidzayiwala,
ndionetseni ndipo ndidzakumbukira,
loleni ndichite nawo ndipo ndidzamvetsetsa."

## Zophunzitsa Nthawiyabaibulo

| | KALASI 0 (sanayambe sukulu)<br>Kalasi Yoyamba (Zaka 5-7)<br>Kalasi Yachiwiri (Zaka 8-10) | Kalasi Yachitatu<br>(Zaka 11-13) | Kalasi Yachinayi<br>(Zaka 14+) |
|---|---|---|---|
| MAPHUNZIRO A | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Abrahamu<br>6. Abrahamu<br>7. Petro<br>8. Petro<br>9. Yakobo<br>10. Akhristu Oyambirira<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Pemphero<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe ndi Kugwa<br>2. Zochitika Zoyamba - Genesis<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Moyo wa Chikhristu<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO B | 1. Moyo Woyambirira wa Khristu<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Mafanizo<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Alembi a Uthenga Wabwino<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yakobo ndi Banja Lake<br>7. Yosefe<br>8. Machitidwe 2:42 - Zoyenera Kuchita<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Lamulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO C | 1. Danieli<br>2. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>3. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute ndi Samueli<br>6. Davide<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Yona<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>3. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Amene Mulungu Anawagwiritsa Ntchito - Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Zoyankhula za Yesu<br>3. Mphamvu za Ambuye<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Ena a mu Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |

## B1 Nkhani Yoyamba

**Kuyamika m'Nyumba ya Mulungu – Iyi ndi nkhani ya kunena "zikomo" kwa Mulungu chifukwa cha Mwana wake.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Mwana Yesu anabadwa kuti akhale Chipulumutso cha Mulungu.<br>• Tikuyenera kunena zikomo kwa Mulungu chifukwa chotipatsa Mwana wake kukhala Mpulumutsi wathu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 2:30***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 2:22-38*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za kulandira mphatso. Funsani ana atchule chinthu chimene analandira chomwe chinawasangalatsa kwambiri. Tsindikani kufunika konena "Zikomo" akalandira mphatso ngakhale itakhala yaying'ono.<br>M'nkhani iyi tikupeza anthu amene anathokoza kwa Mulungu chifukwa cha mphatso yayikulu kwambiri, Ambuye Yesu. |
| **PHUNZITSANI** | • Lero linali tsiku lopambana kwambiri kwa Mariya ndi Yosefe. Iwo anabwera ndi khanda Yesu ku Nyumba ya Mulungu ku Yerusalemu kudzathokoza Mulungu. ***(Luka 2:22-24)***<br>• Iwo ali kumeneko, munthu wokalamba wotchedwa Simeoni anabwera. Iye ankadziwa chokonzero cha Mulungu chotumiza Mpulumutsi – kunena zoona iye analonjezedwa kuti sadzafa asanaone Ambuye Yesu. Mzimu Woyera anamutsogolera Simeoni kuti akumane ndi Mariya ndi Yosefe tsiku limeneli! Simeoni ankadziwa kusintha kumene mwana wapadera ameneyu adzabweretsa pa dziko lapansi. Iye ankadziwa kuti Ambuye Yesu anali mphatso yapadera kwambiri. *Fufuzani zomwe Simeoni ankamva mu mtima mwake pamene ananyamula khandalo m'manja mwake ndi kuyamika Mulungu.* ***(Luka 2:25-35)***<br>• Mayi winanso wokalamba wotchedwa Anna anakumana ndi Mariya ndi Yosefe ali ndi khanda Yesu. Iyenso anayamika Mulungu chifukwa cha Iye. Kenaka anayankhula za Yesu kwa aliyense amene anakumana naye. ***(Luka 2:36-38)*** *Monga Anna, tikuyenera kufuna kugawana ndi ena nkhani yabwino ya kubadwa kwa Yesu!*<br><br>*Ndi anthu angati amene ananena "Zikomo" m'Nyumba ya Mulungu? Werengani ndi kutchula mayina awo. N'kofunika kwambiri kwa ife kuti tithokoze Mulungu chifukwa cha Ambuye Yesu. Nthawi zonse Simeoni ali moyo ankayembekezera tsiku limene Yesu adzabadwa. Ife titha kuyang'ana m'mbuyo ndi kuthokoza chifukwa cha kubadwa kwa Yesu ndi kutinso anakhala Mpulumutsi wathu pamene anafa pa mtanda chifukwa cha machimo athu. Limbikitsani ana kuti azindikire kupambana kwa mphatso ya Mulungu kuposa mphatso zina ndi kuwathandiza kuti azithokoza Mulungu chifukwa cha Ambuye Yesu ndi zonse zimene anatichitira.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjera A – Kuyamika m'Nyumba ya Mulungu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Luka 2:30***. Fotokozani kuti mawu awa ndi gawo la pemphero la Simeoni la kuti "Zikomo". Ambuye Yesu amatipatsa chipulumutso akachotsa machimo athu. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa ngati njira yobwereza nkhaniyi.<br>• Kodi Nyumba ya Mulungu inali kuti?<br>• N'chifukwa chiyani Mariya ndi Yosefe anali kumeneko?<br>• Kodi munthu wokalamba amene anabwera kwa iwo anali ndani?<br>• Kodi Simeoni analonjezedwa chiyani?<br>• Kodi mayi wokalamba amene anathokoza chifukwa cha Yesu anali ndani?<br>• Kodi Anna anachita chiyani ataona khanda Yesu?<br>• Kodi tingaphunzire chiyani kuchokera kwa Simeoni ndi Anna?<br>• Kodi ndi m'buku liti lomwe tikuwerenga za Simeoni ndi Anna? |

## B1 Nkhani Yachiwiri

**Kukula mu Nazarete – Iyi ndi nkhani ya kukula kwa Yesu kukhala mnyamata.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Ali mnyamata, Yesu anaonetsa kuti anali Mwana wa Mulungu.<br>• N'zofunika kutsatira chitsanzo cha Yesu pokhala womvera.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 2:40 (kapena Aefeso 6:1)***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 2:39-52*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za kusochera kapena kusiyana ndi makolo. Zinachitika motani ndipo kuti? Khazikikani pa zomwe makolo ankamva mu mtima mwawo.<br><u>Kapena</u><br>Ngati n'zoyenera, yankhulani za kupita kutali ndi kwanu ndi chisangalalo chake. Fotokozani kuti m'nkhani ya lero Mariya ndi Yosefe anapita ndi Yesu ku mwambo wapadera kutali ndi ku nyumba kwawo. |
| **PHUNZITSANI** | • Yesu anali ku Yerusalemu ndi makolo ake pa Chikondwerero cha Paskha. *(Kwa ana akulu amene akudziwa Baibulo, awuzeni kufunika kwake.) Fotokozerani ana kutalika kwa ulendo umenewu (makilomita 113 ku Yerusalemu kukafika ku Nazarete) pofanizira ndi mtunda umene akuudziwa ndi kuti ankayenda wapansi. Kambiranani kuti kwa Yesu chinali chinthu chosangalatsa kwambiri popeza anali ndi zaka 12 – gulu la anthu, abwenzi awo, ndi mwayi wokaona Nyumba ya Mulungu kumene aphunzitsi ankayankhula za Atate wake Mulungu.* ***(Luka 2:42)***<br>• Atayenda tsiku loyamba kubwerera kwawo, Mariya ndi Yosefe anazindikira kuti Yesu wasowa! *Ganizani zomwe ankamva mu mtima mwawo ndi momwe iwo ankachitira pomufunafuna m'gulu la anthu kenaka ndi kuganiza zobwerera ku Yerusalemu.* ***(Luka 2:43-45)***<br>• Patapita masiku atatu anamupeza Yesu ali m'Nyumba ya Mulungu atakhala pakati pa aphunzitsi. *Fotokozani za chisangalalo chawo ndipo fananizani ndi mawu athu oyamba aja.* Iye akumvetsera ndi kufunsa mafunso, aphunzitsi anadabwa poona kuti ankadziwa zambiri za Mulungu. Mariya ndi Yosefe nawo anadabwanso kwambiri! *Fananitsani zokambirana za Mariya ndi Yosefe ndi kufotokoza kuti ngakhale nthawi imeneyi ali mnyamata ankagwira ntchito ya Atate ake m'Nyumba mwake (Nyumba ya Mulungu).* Mariya ndi Yosefe zinawavuta kuti amvetse kwathunthu zimene Yesu ankayankhula. ***(Luka 2:46-50)***<br>• Izi zitapita, Yesu anabwerera ku Nazarete pamodzi ndi Mariya ndi Yosefe. Iye anamvera iwo m'njira iliyonse, kuwasangalatsa komanso Mulungu Atate ake. *Baibulo likutiwuza kuti tikuyenera kumvera makolo athu.* ***(Aefeso 6:1)*** *Pochita zomwe tawuzidwa tikutsatira zochita za Yesu.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kukula mu Nazarete |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Luka 2:40 (kapena Aefeso 6:1).*** Fotokozani kuti akunena makulidwe osiyanasiyana a Yesu. Ifenso titha kukula motero – kuposa zonse, Mulungu akufuna kuti tikule ndi kukhala anthu omukonda ndi kumutumikira. |
| **KUMBUKIRANI** | <u>Lembani zoona/zabodza pa mawu awa.</u><br>• Phwando la Paskha linali ku Yerusalemu.<br>• Yesu anali ndi zaka khumi pamene izi zinachitika.<br>• Mariya ndi Yosefe anamupeze Yesu patapita tsiku limodzi.<br>• Yesu anali m'nyumba ya m'bale wake.<br>• Mariya anawuza Yesu kuti iwo anali ndi nkhawa.<br>• Yesu ankagwira ntchito ya Atate ake.<br>• Mulungu ndi Atate a Ambuye Yesu.<br>• Yesu anabwerera ku Yerusalemu ndi kukhala womvera Mariya ndi Yosefe. |

<u>B1 Nkhani Yachitatu</u>

**Kubatizidwa mu Mtsinje wa Yordano – Iyi ndi nkhani ya Yesu kubatizidwa ndi Yohane.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yesu analibe tchimo ndipo ankakondweretsa Atate ake nthawi zonse.<br>• Ife ndi ochimwa ndipo tikuyenera kulapa machimo athu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 3:22***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 3:1-22*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za anthu amene amasonkhanitsa gulu la anthu – monga, mafumu, mtsogoleri wa dziko, nduna yayikulu, munthu wamalonda mu msika, wochita zosangalatsa. Aliyense amafuna kuona zomwe zikuchitika kapena kumva zimene akuyankhula. Si zinali zosiyana ndi Yohane pamene anayamba kulalikira m'mbali mwa Mtsinje wa Yordano. Gulu la anthu linasonkhana kudzamva zomwe munthu wodabwitsayu amene ankakhala m'chipululu ankayankhula. ***(Mateyu 3:4)*** |
| **PHUNZITSANI** | • Yohane anali mneneri. Izi zikutanthauza kuti Yohane anali ndi uthenga wofunika kwambiri wochokera kwa Mulungu. Iye ankawauza anthu kuti anali ochimwa ndipo ankayenera kumva chisoni chifukwa cha zolakwa zawo ndi kuzisiya. *(Uku ndiye timati kutembenuka mtima.)* Kenaka iwo ankabatizidwa pomizidwa m'madzi mu Mtsinje wa Yordano. Kutero kunkasonyeza kuti akufuna kusintha njira zawo. ***(Luka 3:2-3, 7)*** *Ngati anaonapo ubatizo wa Chikhristu, fotokozani izi kuti amvetse zomwe anaonazo. Fotokozani kuti tonse tikuyenera kumva chisoni (kulapa) chifukwa cha zoyipa zimene timachita.*<br>• Anthu sankadziwa kuti Yohane anali ndani. Kodi iye ndi amene Mulungu analonjeza kuti adzamutumiza? Yohane anafotokoza kuti wina wamphamvu kuposa iye akubwera. ***(Luka 3:15 ndi 16)*** *Kodi iyeyu ndi ndani?*<br>• Kenaka tsiku lina Ambuye Yesu anafika pamodzi ndi anthu ena ndipo anabatizidwa. *Kodi Yesu sankayenera kuchita chiyani asanabatizidwe? Kambiranani kuti Yesu anali wosiyana ndi munthu wina aliyense (ndi ifenso) popeza Iye analibe tchimo ndipo sankayenera kulapa.* Koma Yesu anafuna kuonetsa kuti anali munthu ngati ife, kuti nayenso akuyenera kuchita zomwe Mulungu ananena. Yesu atabatizidwa, chinachake chodabwitsa chinachitika. Mulungu anayankhula Kumwamba, kunena kuti anali wokondwa kwambiri ndi Mwana wake ndipo Mzimu Woyera anabwera pa Iye monga nkhunda. ***(Luka 3: 21-22)*** *N'chifukwa chiyani Mulungu anakondwera ndi Ambuye Yesu?*<br>• *Ife sitingakondweretse Mulungu m'njira imene Yesu anachita. Koma Mulungu amakondwera ngati tamva chisoni chifukwa cha machimo athu (kulapa) ndi kusankha kukhala moyo wokondweretsa Iye.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kubatizidwa mu Mtsinje wa Yordano. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Luka 3: 22 (gawo b).*** Funsani mafunso osavuta kuti muone ngati ana amvetsetsa nkhaniyi. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa monga njira yobwereza nkhani imeneyi.<br>• Kodi Yohane ankalalikira kuti?<br>• Kodi Yohane anautenga kuti uthenga wake?<br>• Yohane anawuza anthu kuti "alape". Kodi zikutanthauza chiyani?<br>• Kodi Yohane ankachita chiyani kwa anthu amene ankalapa?<br>• Kodi Yohane anafotokoza zotani za munthu amene ankayenera kubwera pambuyo pake?<br>• Kodi Yesu anafuna kuti Yohane achite chiyani?<br>• Kodi kubatizidwa kwa Yesu kunali kosiyana motani ndi kubatizidwa kwa anthu ena?<br>• Kodi ife tingakondweretse Mulungu motani? |

## B1 Nkhani Yachinayi

**Kuyesedwa m'chipululu – Iyi ndi nkhani yonena kuti "Ayi" pa zinthu zolakwika.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Ambuye Yesu sanachimwepo.<br>• Iye angathe kutithandiza pamene tikuyesedwa kuti tichite zolakwa.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 4:8***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 4:1-13*** |
| **MAWU OYAMBA** | Apatseni ana chitsanzo cha mayesero choyenerana ndi msinkhu wawo. (Onani chitsanzo poyamba pa phunziro la Kalasi 2.) Yankhulani za momwe angaperewere mayesero. Lero tiphunzira zomwe Yesu anachita pamene ankayesedwa. |
| **PHUNZITSANI** | • Yesu atabatizidwa Mzimu Woyera anamutsogolera ku chipululu. *Kambiranani za kukhala m'chipululu masiku makumi anayi – kutentha, kuuma, kukhala wekha ... Pezani chitsanzo chabwino chomwe chingathandize ana kuti amvetsetse za kutalika kwa masiku makumi anayi.* ***(Luka 4:1-2)***<br>• Yesu sanadye kanthu, choncho anali ndi njala kwambiri! Kuposa china chilichonse, Iye ankafuna chakudya. *Nenani mawu amene mdierekezi anayankhula kwa Yesu.* Iyi ikanakhala njira yosavuta kuti Yesu akhale ndi chakudya! Koma Yesu anayankha pogwiritsa ntchito Mawu a Mulungu amene anaonetsa kuti mawu a mdierekezi anali olakwika. ***(Luka 4:3-4)***<br>• Mdierekezi anabweranso kwa Yesu ndi kumutenga kupita naye pa phiri lalitali pamene anamuonetsa maufumu onse a dziko lapansi. Iye anati ngati Yesu angamugwadire, zonsezo zidzakhala zake - adzamupatsa. Yesu anayankha kuti, "Zalembedwa: 'Pembedza Yehova Mulungu wako ndi kumutumikira Iye yekha.'" Nthawi yachiwiri, Yesu akugwiritsa ntchito mawu a m'Baibulo kuonetsa mdierekezi kuti zomwe akunenazo ndi zolakwika. ***(Luka 4:5-8)***<br>• Pomaliza, mdierekezi anatenga Yesu ndi kupita naye pamwamba pa Nyumba ya Mulungu mu Yerusalemu. Iye anamuwuza kuti ngati ndi Mwana wa Mulungu, adzigwetse pansi ndipo sadzavulala. Iye ankayesa Yesu kuti aonetse mphamvu zake. Koma Yesu anadziwa kuti kutero ndi kulakwa ndipo anamuyankha mdierekezi pogwiritsanso mawu ochokera m'Baibulo. Nthawi imeneyi mdierekezi anamusiya Yesu yekha. ***(Luka 4:9-13)*** *N'chifukwa chiyani mdierekezi anachoka? Nanga akanapambana? Kodi Yesu anagonjetsa mayeserowa motani?*<br>• *Tsirizani ponena kuti Ambuye Yesu sanachimwepo. Iye ndi wamphamvu kuposa mdierekezi. Iye anagwiritsa ntchito Mawu a Mulungu kusonyeza kuti ankamvera Atate ake Mulungu. Ngati ndife a Ambuye Yesu, adzatithandiza kuyankha kuti "AYI" pa zinthu zolakwika. Ngati timadziwa Mawu a Mulungu ngati Ambuye Yesu, titha kuwagwiritsa ntchito kuti tipeze mphamvu zochitira zolondola.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuyesedwa m'chipululu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Luka 4:8***. Fufuzani ngati ana akukumbukira zochitika pomwe vesiyi yachokera. Kodi anayankhula ndi ndani? Amayankhula kwa ndani? N'chifukwa chiyani Yesu anagwiritsa ntchito mawu amenewa? |
| **KUMBUKIRANI** | M'malo mwa mafunso, gwiritsani ntchito "kuganiza kwambiri" pofuna kudziwa zonse zimene ana aphunzira za Ambuye Yesu mu B1. Mphunzitsi alemba maganizo (akhale aafupi kapena mwachidule) pa pepala lalikulu. Ana okulirapo achite izi m'magulu kenaka adzafotokoze kwa m'phunzitsi. |

## B2 Nkhani Yoyamba

**Yesu asandutsa madzi kukhala vinyo – Iyi ndi nkhani ya Yesu ku ukwati.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yesu anachita chodabwitsa ichi chifukwa ndi Mwana wa Mulungu.<br>• Ife tikuyenera kumumvera monga anachitira antchitowa.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 2:5***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Yohane 2:1-11*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani zomwe zimachitika pa ukwati kwanuko. Aloleni ana afotokoze zomwe akudziwa. Pezani zinthuzi zingapo ngati zilipo. Nanga mungatani zinthu zitakhala kuti sizikuyenda bwino pa ukwatiwo? Perekani chitsanzo chimodzi kapena ziwiri.<br>M'nkhani yathu lero, Yesu ndi ophunzira ake pamodzi ndi amayi, Mariya, anali alendo pa ukwati ku Kana. ***(Yohane 2:1-2)*** Tiyeni tione zomwe zinachitika. |
| **PHUNZITSANI** | • *Fotokozani zochitika – mkwati ndi mkwatibwi osangalala, alendo, akuyankhula ndi kuseka, chakudya chokoma ndi zakumwa, aliyense akusangalala pa ukwatiwo.* Koma Mariya anazindikira kuti china chake sichinali bwino – vinyo anali atatha! *Kodi mkwati ndi mkwatibwi anamva bwanji m'mitima mwawo?* Mariya anadziwa choyenera kuchita. Nthawi yomweyo anafotokozera Yesu. *Fotokozani kuti Yesu ndiye angathe kuchotsa mavuto athu. Titha kupemphera kwa Iye.* Kenaka iye anatembenukira kwa antchito ndi kuti, "Inu muchite chilichonse chimene akuwuzeni." Mariya ankadziwa kuti Yesu akanatha kuthandiza. Iye ankamudalira kwathunthu. ***(Yohane 2:3-5)***<br>• *Fotokozani kuti m'chipindamo munali mitsuko yayikulu ya miyala isanu ndi umodzi (uliwonse unali wautali 1 mita) m'mene ankasungira madzi ophikira kapena oti anthu azisamba m'manja.* Yesu anawuza antchito aja kuti adzaze madzi mitsukoyo ndi kutungamo kukapereka kwa woyang'anira ukwatiwo. *Fotokozani kuti izi zinali za chilendo kwambiri...* Awa anali madzitu? Koma iwo anamvera Yesu ndipo anadabwa poona madzi aja atasintha. Anali vinyo! Kunena zoona, onse anavomereza kuti anali vinyo OKOMA KWAMBIRI, kuposa amene anali naye poyamba. ***(Yohane 2:6-10)*** *Nthawi zonse Ambuye Yesu amapereka zinthu zabwino!*<br>• *Fotokozani kuti ichi chinali chodabwitsa. Palibe akanatha kuchita zomwe Yesu anachita. Iye anachita izi chifukwa ndi Mwana wa Mulungu, Mlengi wa zinthu zonse.*<br>• *N'zofunika kwambiri kuti antchito anamvera Yesu. Afunse ana aganize zomwe zikanachitika ngati sakanamvera. Yankhulani za vuto lomwe tili nalo – tchimo lathu. Yesu ali ndi yankho la vuto lathu chifukwa Iye anafa pa mtanda kulangidwa m'malo mwa tchimo lathu. Koma ndi pamene tamukhulupirira pamene Iye angachite chodabwitsa m'miyoyo yathu ndi kutikhululukira tchimo lathu.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Yesu asandutsa madzi kukhala vinyo. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Yohane 2:5***. Fotokozani zomwe zikuchitika m'nkhaniyi. Fufuzani kuti mudziwe ngati ana akudziwa kuti "Iye" ndi ndani. Ana aang'ono aphunzira gawo lachiwiri la vesili. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani imeneyi.<br>• Kodi ukwati unali kuti?<br>• Tchulani mayina a anthu ena pa ukwatiwo.<br>• Ndi ndani amene anawuza antchito kuti amvere Yesu?<br>• Kodi Yesu anawuza antchito kuti achite chiyani?<br>• Kodi panali mitsuko ingati ya madzi pamenepo?<br>• Kodi chinachitika ndi chiyani antchito atatunga madzi aja mu mitsuko?<br>• Kodi aliyense anagwirizana kuti chiyani?<br>• N'chifukwa chiyani Yesu anatha kuchita chodabwitsa ichi?<br>• Kodi vuto la miyoyo yathu ndi chiyani?<br>• Kodi tikuphunzira chiyani kuchokera kwa antchito amenewa? |

## B2 Nkhani Yachiwiri
## Yesu achiritsa mnyamata wodwala – Iyi ndi nkhani ya mphamvu ya Yesu.

**Ife tikuphunzira kuti:**
- Yesu anali ndi mphamvu zochiritsa chifukwa ndi Mwana wa Mulungu.
- Yesu akufuna ife timukhulupirire monga inachitira nduna ya boma iyi.

**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 4:50***
**Ndime Yowerenga:** ***Yohane 4:46-54***

**MAWU OYAMBA**

Bwerezani nkhani ya sabata latha. Kodi ku ukwati kunachitika chiyani? Kodi ukwati unali kuti? Yankhulani za kuti nkhani ya chodabwitsa ichi inafala ku Kana ndi kumadera ozungulira. Nduna ya mfumu mu nkhani ya lero mwina anamva zonse zimene Yesu ankachita.

**PHUNZITSANI**

- Nthawi ina Yesu anabweranso ku Kana. Ku tawuni yoyandikana nayo ya Kapernao, munthu wolemekezeka (nduna ya mfumu) anamva zomwe Yesu anachita ku Kana. Ndi Yesu yekha akanatha kumuthandiza! Mwana wake wa mwamuna ankadwala kwambiri. Ndunayi inaganiza kuti ngati Yesu atabwera ku nyumba kwake, Iye adzachiritsa mwana wakeyo. ***(Yohane 4:47)*** *Kwa ana a Kalasi 2 mutha kungowaonetsa mapu a matawuni awiri amenewa.*
- Ndunayi inayenda makilomita 32 kuti ikafike komwe kunali Yesu. *Taganizani momwe iyo inkamvera – inali yotopa, ya nkhawa, yothedwa nzeru...* Iyo inapempha Yesu kuti apite nayo kwawo. Pamene inamuwuza za mwana wake wamwamuna, Yesu anayiwuza kuti ipite kwawo ndipo mwana wake adzakhala ndi moyo. Yesu sanakapita nayo kwawo! *Ganizirani momwe inachitira ndipo kenaka fotokozani kuti iyo inakhulupirira mawu a Yesu. Iyo inali ndi chikhulupiriro mwa Yesu kuti sikunali kofunika kuti ayende makilomita 32 kuti akachiritse mwana wake.* ***(Yohane 4:47-50)*** *Fotokozani kuti Yesu akufuna chikhulupiriro chotere mwa ifenso. Ife sitingamuone kapena kumva mawu ake koma malonjezo ake m'Mawu ake, m'Baibulo, akuti Iye amatikonda ndipo akufuna kuti atikhululukire.*
- Pamene munthuyo ankayenda kubwerera kwawo, antchito ake anakumana naye ali ndi nkhani yabwino. *Funsani ana kuti aganize kuti nkhani yabwinoyi inali yotani.* Inde! Mwana wake anachira... ndipo pamene anafunsa za nthawi yomwe anachira, iye anazindikira kuti inali nthawi yomwe Yesu anamuwuza kuti mwana wake adzakhala ndi moyo. Banja lake linali ndi chisangalalo chotani! Anthu onse anatsimikiza kuti Yesu anali chimene Iye ankanena kuti anali – Mwana wa Mulungu. ***(Yohane 4:51-53)***
- Ifenso tikuyenera kukhulupirira kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Iye akufuna kuti ife timukhulupirire. Pamenepo tidzakhala osangalala kwenikweni.

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Yesu achiritsa mnyamata wodwala.

**PHUNZIRANI**

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Yohane 4:50***. Tsindikani tanthauzo la "kukhulupirira mawu" ake.

**KUMBUKIRANI**

Funsani ana mafunso awa monga njira yobwereza nkhaniyi.
- Kodi vuto la ndunayi linali chiyani?
- Kodi iyo inakamupeza Yesu kuti?
- Kodi iyo inayenda makilomita angati?
- Kodi Yesu anayiwuza kuti ichite chiyani?
- Iyo inakumana ndi ndani pamene inkabwerera kwawo?
- Kodi anabweretsa uthenga otani?
- Kodi mwana anachira nthawi yanji?
- Lembani mawu amene palibe – "Ndunayi ________ Yesu kwathunthu".

## B2 Nkhani Yachitatu

**Yesu ndi Bartimeyu – Iyi ndi nkhani ya kuchiritsidwa kwa munthu wosaona amene anayamba kutsatira Yesu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Ambuye Yesu ankafuna kuthandiza Bartimeyu ndipo anali ndi mphamvu zosintha moyo wake.<br>• Yesu akufuna kusintha miyoyo yathu potichotsera machimo athu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Marko 10:52***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Marko 10:46-52*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za mphatso yabwino ya kuona - kuona mitundu yosiyanasiyana, kusangalala ndi malo abwino, kuzindikira anthu, kuwerenga mabuku, kuchita masewero, kuonera kanema ndi zina zambiri. Mwanzeru kambiranani za kukhala wosaona lero. Fotokozani kuti nthawi ya Yesu, moyo wa munthu wosaona unali wovuta kwambiri. |
| **PHUNZITSANI** | • Bartimeyu anali munthu wosaona amene ankakhala mu Yeriko. Kwa iye tsiku lililonse linalo lofanana - kupempha m'mbali mwa msewu kuti akhale ndi moyo. Koma lero linali tsiku losiyana. *Fotokozani za phokoso la anthu ndi kuti Bartimeyu wadziwa kuti Yesu akubwera.* Nthawi yomweyo Bartimeyu anayamba kusangalala! Iye anali atamva zomwe Yesu ankachita. *Kodi mukuganiza kuti iye ankafuna kuti Yesu amuchitire chiyani?* Bartimeyu anayamba kufuula, kupempha thandizo kwa Yesu. Anthu ena anakwiya naye ndipo anamuwuza kuti akhale chete koma iye anapitiriza kufuula kwambiri! ***(Marko 10: 46-48)*** *Fotokozani kuti Bartimeyu ankachita chinthu choyenera chifukwa ndi Yesu yekha amene akanatha kumuchiritsa kuti aonenso. Ndi Ambuye Yesu wokha amene angatikhululukire machimo athu. Monga Bartimeyu ankayenera kukumana ndi Ambuye Yesu, ifenso tikufuna thandizo lake.*<br>• Nthawi imeneyi Yesu anayima ndi kuwuza munthu wina kuti amuyitane Bartimeyu abwere kumene kunali Iye. *Fotokozani momwe anayankhira Bartimeyu. Kodi tsopano Bartimeyu akumva chiyani mu mtima mwake?* Yesu anamufunsa chimene ankafuna ndipo anayankha kuti akufuna kuonanso. Yesu anamuwuza kuti apite ndipo chikhulupiriro chake chamuchiritsa. Nthawi yomweyo, Bartimeyu anayamba kuona! *Funsani ana kuti aganize chomwe iye anayamba kuchiona pamene analipo. Fotokozani maganizo ake ndi za kutsatira Yesu kumene anachita pa msewupo.* ***(Marko 10:49-52)***<br>• *Bartimeyu sakanayiwala tsiku limene anakumana ndi Yesu. Yesu anachita chodabwitsa pa iye ndipo moyo wake unasintha! Fotokozani kuti Ambuye Yesu akufuna kuchita chodabwitsa chachikulu pa ife posintha miyoyo yathu ndi kuchotsa tchimo lathu. Pamene tibwera kwa Iye ndi kumukhulupirira tidzapeza chimwemwe chenicheni monga anachipeza Bartimeyu.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Yesu ndi Bartimeyu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Marko 10:52***. Fotokozani kuti "chikhulupiriro" cha Bartimeyu ndiye kunali kudalira kwake Ambuye Yesu. Iye ankadziwa kuti Yesu anali ndi mphamvu yomupatsa kuona kwake. Yesu akufuna ife tikhale ndi chikhulupiriro mwa Iye. Vesi ina yomwe mungaloweze nso ndi ***Yohane 8:12-gawo b***. |
| **KUMBUKIRANI** | Lembani zoona kapena zabodza pa mawu awa.<br>• Bartimeyu anali ku Kana.<br>• Iye anali wosaona.<br>• Iye anali wosayankhula.<br>• Panali anthu ambiri amene ankafuna kuona Yesu.<br>• Bartimeyu anakhala chete pamene anthu anamuletsa kufuula.<br>• Yesu anakhala ngati sakumva.<br>• Bartimeyu anayimirira ndi kupita kumene kunali Yesu.<br>• Gulu linamutchinga kuti asathe kufika kumene kunali Yesu.<br>• Bartimeyu anapitiriza kupempha atakumana ndi Yesu.<br>• Ambuye Yesu atha kuchita chodabwitsa kwa aliyense wa ife. |

## B2 Nkhani Yachinayi
## Yesu achiritsa anthu akhate khumi – Iyi ndi nkhani ya kunena "Zikomo" kwa Yesu.

**Ife tikuphunzira kuti:**

- Anthu akhate anamvera Yesu ndipo anachiritsidwa.
- Ambuye Yesu akufuna kuti ife tizimuthokoza chifukwa cha ubwino wake pa ife.

**Vesi Yoloweza:** ***Salimo 107:21***
**Ndime Yowerenga:** ***Luka 17:11-19***

### MAWU OYAMBA

Yankhulani za kukhala wothokoza. Funsani ana aganizire zinthu zomwe akuyenera kukhala oyamika tsiku lililonse (monga: chakudya, madzi, nyumba, thanzi, banja, sukulu) ndipo lembani zimenezo. Fotokozani kuti Mulungu ndiye amapereka zinthu zonse zabwino zomwe timasangalala nazo ndipo yambani ndi pemphero la kuyamika, ndi kukumbukira amene alibe zimenezi.

### PHUNZITSANI

- Nkhani ya lero ndi ya amuna khumi amene ankakhala moyo ovutika. *Fotokozani momwe khate linakhudzira moyo wawo – onani mawu oyamba mu Nthawiyabaibulo Kalasi 1 kapena 2.*
- Koma tsiku lina china chake chosangalatsa chinachitika. Yesu anali kudera kumene iwo ankakhala. Ngakhale sankaloledwa kuyandikira munthu wina aliyense, iwo anamuona Iye ali patali ndipo anadziwa kuti Yesu atha kuwathandiza. Onse pamodzi anayitana Yesu mokweza mawu kuti, "Yesu, Ambuye, tichitireni chifundo!" ***(Luka 17:11-13)***
- Yesu anamva ndipo anawayitana ndi kuwawuza kuti, "Pitani kadzionetseni nokha kwa ansembe." *Fotokozani kuti m'Malamulo ananena kuti aliyense amene wachira nthenda ya khate akuyenera kupita kwa wansembe kuti akamuone ngati wachiradi.* Anthuwa anazindikira kuti Yesu awachiritsa chonse nthawi yomweyo anamvera Yesu ndi kunyamuka kumapita. Ndipo pamene ankapita, mwadzidzidzi khate linachoka pa matupi awo! Yesu anali atawachiritsa. *Kodi iwo anamva bwanji m'mitima mwawo?* ***(Luka 17:14)*** *Iwo anachita choyenera kumvera Yesu. Ifenso tikuyenera kudalira ndi kumvera Iye ngati tikufuna kudalitsidwa kapena kulandira zabwino kuchokera kwa Iye.*
- Anthu khumi aja anadabwa kwambiri kuona kuti kusinthika kodabwitsa kwachitika pa iwo komatu ndi mmodzi yekha amene anabwerera kudzanena "zikomo". Pamene ankayamika Mulungu chifukwa cha zomwe zachitika, iye anabwerera msanga ndi kupita komwe kunali Yesu ndi kugwa pansi pa mapazi a Yesu. *Fotokozani kuti munthu uyu anali wosiyana ndi ena chifukwa anali Msamariya ndipo samachokera m'dziko lomwe Yesu ndi enawo amachokera.* Yesu anakondwera kwambiri kuti munthu uyu anali woyamika ndi anamuyamikira chifukwa choonetsa chikhulupiriro pamene anamvera. *Kodi mukuganiza kuti Yesu anamva bwanji mu mtima mwake chifukwa cha ena asanu ndi anayi aja?* ***(Luka 17:15-19)*** *Kodi mukuganiza ndi munthu uti amene anali wokondwa kwambiri tsiku limeneli?*
- *Ife tikuyenera kukhala oyamika Mulungu (kumbutsani ana zomwe analemba zija) ndiponso Ambuye Yesu amene anapereka moyo wawo kuti machimo athu akhululukidwe. Limbikitsani ana kuti atsatire chitsanzo chabwino cha munthu m'nkhani imeneyi.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A –Yesu achiritsa anthu akhate khumi.

### PHUNZIRANI

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Salimo 107:21***. Fotokozani mawu achilendo – monga: chifundo, zodabwitsa.

### KUMBUKIRANI

M'malo mokhala ndi mafunso, ana akhale awiriawiri ndipo ajambule chithunzi chosonyeza kuyamika. Ana ena achekenire mawu akuti ZIKOMO MULUNGU pakati pa zithunzizo.

Gulu la ana aang'ono litha kujambula zinthu khumi zoyimira akhate khumi aja.

1. Tengani pepala ndi kulipindapinda zigawo khumi.
2. Jambula munthu pamwamba pa gawo lililonse ndipo manja ake afike kumapeto kwake.
3. Dulani mozungulira kuti pakhale akhate khumi koma olumikizana.

## B3 Nkhani Yoyamba

**Kuphunzitsidwa ndi Yesu – Iyi ndi nkhani ya kukhala ndi nthawi yophunzitsidwa ndi Yesu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Kumvetsera zomwe Yesu akuyankhula ndi kuphunzira kuchokera kwa Iye ndi zofunika kwambiri.<br>• Tikuyenera kumvetsera zomwe Yesu akuyankhula kudzera m'Baibulo.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 10:42***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 10:38-42*** |
| **MAWU OYAMBA** | Sankhani fundo imodzi:<br>• Yankhulani za momwe amayi anu angakonzekere pofuna kulandira alendo m'nyumba mwanu – kuphika chakudya ndi zina.<br>• Yankhulani nkhani ya tanthauzo kwa ana - pomwe ndi pofunika kumvetsera – kuphunzira luso latsopano, kupatsidwa malangizo....<br>• Ndi gulu lochepa chitani sewero la 'Long'onezana'. Mtsogoleri apereke uthenga monong'ona kwa munthu woyamba ndipo munthuyo anong'oneze wina mawu omwewo ndipo amene wang'onezedwa anong'onezenso mnzake. Munthu womaliza ayankhule zomwe anamva. Sewero limaonetsa kufunika kokhala womvetsera wabwino. Lumikizani ndi nkhani ya lero imene ndi ya munthu amene akukhala ndi nthawi yomvera mwachidwi. |
| **PHUNZITSANI** | • Marita ndi Mariya anali abwenzi abwino a Yesu. Tsiku lina Marita anayitana Yesu ndi ophunzira ake kuti adzadye. *Funsani ana kuti aganizire zomwe iye anakonzekera kapena mulumikize ndi fundo yoyamba yomwe ili pamwambayi. Onani kufika kwa alendo.* ***(Luka 10:38)***<br>• Marita anali ndi zambiri zoti achite! Pamene ankakonzekera chakudya, mchemwali wake, Mariya, anali atakhala pansi pa mapazi a Yesu kuphunzira kuchokera pa zomwe ankayankhula. *Fotokozani momwe Marita ankamvera mu mtima mwake... mwina ana angamvetse zimenezi! Gwiritsani ntchito mawu enieni amene Marita anayankhula.* ***(Luka 10:39-40)***<br>• Yesu anayankhula mwaulemu kwa Marita, kunena kuti sankayenera kutanganidwa ndi kukhumudwa. *Fotokozani kuti Mariya ankagwira ntchito yabwino yokonzera chakudya chabwino Yesu, koma sichinali chinthu chofunika kwambiri nthawi imeneyo.* Kodi ndi ndani ankachita chinthu chabwino? Inde, anali Mariya! Yesu anawuza Mariya kuti anasankha kuchita chinthu chabwino kwambiri chomwe sichidzachotsedwa kwa iye. ***(Luka 10:41-42)***<br>• *Kodi chinthu chabwino chimene Mariya anasankha chinali chiyani? Mariya anali ndi mwayi waukulu womvetsera zomwe Yesu ankayankhula. Yankhulani zomwe tikuyenera kuchita kuti tikhale ndi nthawi yomvetsera zoyankhula za Yesu pa kuwerenga ndi kuphunzira Baibulo. Tikatero tidzamudziwa bwino komanso kudziwa zomwe zimamukondweretsa. Ndi ana okulirapo mutha kukambirana zomwe iwo angachite kuti izi zikhale zoyamba m'moyo wawo.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuphunzitsidwa ndi Yesu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Luka 10:42***. Tsimikizani kufunika kwa chisankho chimene Mariya anachita. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso otsatiriwa monga njira yobwereza nkhaniyi.<br>• Kodi achemwali ankakhala kuti?<br>• Kodi alendo anali ndani?<br>• Ndi mchemwali uti amene anakhala ndi nthawi pamaso pa Yesu?<br>• Ndi mchemwali uti amene ankafuna kutumikira Yesu?<br>• Kodi ndi mchemwali uti amene anakhumudwa?<br>• Kodi Marita anakwiya chifukwa chiyani?<br>• Kodi Marita anadandaula kwa ndani?<br>• Kodi ife titsatire zochita za mchemwali uti?<br>• Kodi tingamvetsere motani kwa Yesu?<br>• Kodi ndi buku liti m'Baibulo limene nkhani iyi ikupezekamo? |

## B3 Nkhani Yachiwiri

**Moyo kuchokera kwa Yesu – Iyi ndi nkhani ya Yesu kupereka moyo kwa munthu wakufa.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yesu anali ndi mphamvu youkitsa Lazaro.<br>• Yesu atha kutipatsa moyo wosatha pamene tamukhulupirira.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 11:25***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Yohane 11:1-7, 17-44*** |
| **MAWU OYAMBA** | • Kwa ana a Kalasi 1, kambiranani momwe Mulungu amabweretsera anthu m'mabanja. Yankhulani za abale ndi alongo. Kodi ubwino okhala ndi abale/alongo ndi otani? Funsani ana ngati akukumbukira mayina a achemwali awiri mu phunziro la sabata latha ndi kuwawuza za Lazaro.<br>• Kwa ana a Kalasi 2, fotokozani kuti si nthawi zonse zimene zofuna zathu zimakwaniritsidwa – nthawi zina, zosaziyembekezera zimachitika zomwe palibe chimene tingachite. Fotokozani momwe Ambuye Yesu akulamulalira pa nyengo ina iliyonse ndi kuti zotsatira zake zimakhala zabwino kwambiri. Mu nkhani yathu ya lero Mariya ndi Marita anali ndi vuto lalikulu. |
| **PHUNZITSANI** | • Mlongo wa Mariya ndi Marita, Lazaro, ankadwala kwambiri. Iwo ankafuna kuti Yesu abwere, choncho anatumiza uthenga kwa Iye. Iwo ankadziwa kuti Iye akhoza kuchiritsa Lazaro. Koma Yesu anasankha kusabwera! *Kodi iwo anamva bwanji m'mitima mwawo? Fotokozani kuti ngakhale Mariya ndi Marita sanamvetsetse, Ambuye Yesu ankalamulira zochitika ndipo ankadziwa chinthu chabwino choti chichitike.* ***(Yohane 11:1-6)***<br>• Nthawi yomweyo Lazaro anamwalira ndipo anakutidwa mu nsalu ndi kuyikidwa m'manda m'mphanga ndi kutseka ndi mwala waukulu pa khomo lake. Ife timatcha amenewa manda. *Mosamala ganizirani zomwe zinkadutsa m'maganizo a Marita ndi Mariya.* Patatha masiku anayi, Marita anamva kuti Yesu akubwera. Ananyamuka kupita kukakumana naye. Yesu anafotokozera Marita kuti Lazaro adzakhalanso ndi moyo. *Gwiritsani ntchito mawu amene Yesu anayankhula* ***(vesi 25)*** *ndipo fotokozani kuti tanthauzo la kuuka ndi kukhala ndi mphamvu zochititsa munthu wakufa kukhalanso moyo.* Palibe wina aliyense ali ndi mphamvu zimenezi! ***(Yohane 11:17-27)***<br>• Kenaka Yesu anapita ku manda a Lazaro pamodzi ndi Mariya ndi Marita. Yesu analira chifukwa cha chisoni. Kenaka anapempha anthu kuti achotse mwala ndipo anafuula kuti, “Lazaro, tuluka!” Modabwitsa aliyense, Lazaro anatuluka m'manda atakulungidwa ndi nsalu. Apa Yesu anaonetsa kuti anali ndi mphamvu yobwezera moyo kwa Lazaro! Chodabwitsa chimene Yesu anachita chinawathandiza kuti adziwe za mphamvu za Yesu ndi chomwe Iye anali. ***(Yohane 11:33-44)*** *Yankhulani zonse zimene anaphunzitsa kuchokera pa chodabwitsa chimenechi – nthawi yake, kumva chisoni kwawo, mphamvu zake, kulamulira zochitika... Mufotokoze kuti Yesu akanabwera Lazaro asanamwalire, chodabwitsachi sichikanakhala chofunika!*<br>• Ambuye Yesu angathe kugonjetsa m'dani wathu wamkulu kwambiri – imfa. Iye ali ndi mphamvu zogonjetsa imfa, monga anaonetsera pamene anaukitsa Lazaro, komanso pamene Iye mwini anauka kwa akufa. Pamene tadalira Ambuye Yesu, Iye amalonjeza kutipatsa moyo wosatha.<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Moyo kuchokera kwa Yesu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Yohane 11:25***. Fotokozani kuti Yesu akutiphunzitsa kufunika kwake kogwiritsa dzina lino. Ana amene akudziwa Baibulo kwambiri atha kukumbukira pamene pali mawu akuti “Ine Ndine”. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa ngati njira yobwereza nkhaniyi.<br>• Ndani ankadwala kwambiri?<br>• Panatenga nthawi yayitali motani Yesu asanabwere?<br>• Kodi ndi mchemwali uti amene anapita kukakumana ndi Yesu?<br>• Kodi Yesu anadzitcha ndani pamene ankayankhula ndi Marita?<br>• Kodi Yesu anaonetsa motani kukhudzika kwake pa manda a Lazaro?<br>• Kodi anayankhula mawu otani?<br>• Kodi Yesu anatsimikizira chiyani aliyense tsiku limenelo?<br>• Kodi ife tingalandire bwanji moyo wosatha? |

**<u>B3 Nkhani Yachitatu</u>**

**Kukonda Yesu – Iyi ndi nkhani ya Mariya kuonetsera chikondi chake kwa Yesu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Mariya anaonetsa chikondi chake pa Yesu kudzera mu zimene anachita.<br>• Ife tikuyenera kukonda Yesu pobwezera chikondi chake pa ife.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Yohane 4:19***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Yohane 12:1-11*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za 'mphatso za kuthokoza'. Ngati n'kotheka, mupeze mphatso zingapo ngati zitsanzo zomwe mumapereka kwanuko ndipo musankhe amene akuyenera kulandira mphatso zimenezo.<br>Kumbutsani ana nkhani ya sabata latha ya kuthokoza kwa Mariya, Marita ndi Lazaro kwa Yesu. |
| **PHUNZITSANI** | • Mariya, Marita ndi Lazaro anaganiza zochita phwando laulemu kwa Yesu. *Perekani chithunzi – nyumba inadzaza ndi alendo, Lazaro ankaoneka wamphamvu ndi wathanzi, Yesu ndiye anali mlendo wapadera kwambiri, Marita akutumikira...* ***(Yohane 12:1-2)***<br>• Pa phwandoli, Mariya anabwera pamene panali Yesu, atanyamula botolo la mafuta onunkhira amtengowapatali. Nthawi yomweyo anakhuthulira pa mapazi a Yesu ndi kupukuta ndi tsitsi lake. *Fotokozani momwe nkhani yonse pakati pa alendo inali ya Mariya atamva fungo labwino la mafuta onunkhira. Fotokozani kuti Mariya anachita izi chifukwa ankakonda Yesu kwambiri – Iye anali woyenera kwa iye kuposa china chilichonse.* ***(Yohane 12:3)***<br>• Yudase anali mmodzi mwa ophunzira a Yesu ndipo sankamvetsa chifukwa chomwe Mariya anakhuthulira mafuta onunkhira pa Yesu. Kwa iye zinkaoneka kuti akuononga! *Nenani mawu amene Yudase anayankhula ndi kufotokoza kuti Yudase anali wadyera ndi wakuba (Phunziro la Kalasi 2).* ***(Yohane 12:4-6)***<br>• Yudase ndi Mariya anali ndi maganizo osiyana pa Ambuye Yesu. Yudase sankazindikira kupambana kwa Yesu ndipo mu mtima mwake sankakonda Yesu. Koma kwa Mariya, Yesu anali wofunika kwambiri ndipo ankamukonda kwambiri. Yesu anakondwera ndi zomwe anachita Mariya. ***(Yohane 12:7-8)*** *Kodi ife titsatire zochita za ndani?*<br>• *Tikaganiza momwe Ambuye Yesu amatikondera ndi kupereka moyo wake kuti atipulumutse, Iye akuyenera kukhala wopambana kwambiri kwa ife. Titha kumukonda, pobwezera chikondi chake pa ife monga anachitira Mariya. Yankhulani za njira zomwe tingaonetsere chikondi chathu kwa Yesu monga kumukhulupirira, kukhala ndi nthawi yopemphera pamaso pake ndi kuwerenga Mawu ake, kumumvera, kukonda ena ndi kuwuza ena za Iye.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kukonda Yesu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***1 Yohane 4:19***. Onetsetsani kuti ana akumvetsetsa za mawu akuti "Iye" kuti ndi ndani. Fotokozani kuti chikondi chathu ndi chotsatira chikondi chake pa ife. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa ngati njira yobwereza nkhaniyi.<br>• Kodi phwando linali kuti?<br>• Kodi munthu wofunika kwambiri kumeneko anali ndani?<br>• Kodi Mariya anachita chiyani?<br>• N'chifuka chiyani Mariya anachita zimenezi?<br>• Kodi Yudase ananena chiyani pamene Mariya anathira mafuta onunkhira pa Yesu?<br>• N'chifukwa chiyani tikuyenera kukonda Ambuye? |

**B3 Nkhani Yachinayi**

**Kuyang'ana Yesu – Iyi ndi nkhani ya kulandiridwa kwa Yesu.**

<table>
<tr><td></td><td>Ife tikuphunzira kuti:<br>• Yesu ndi wofunika kwambiri – Iye ndi Mfumu ya Mafumu.<br>• Ife tikuyenera kulandira Ambuye Yesu m'miyoyo yathu.<br><br>Vesi Yoloweza: Yohane 1:12<br>Ndime Yowerenga: Luka 19:28-44</td></tr>
<tr><td>MAWU OYAMBA</td><td>Yankhulani za momwe amalandirira mlendo wolemekezeka – monga: mafumu, mtsogoleri wa dziko, katswiri wa masewero, alendo a pa sukulu. Gwiritsani zithunzi ngati zilipo. Yesani kukhala ndi maganizo a momwe zingakhalire ngati mutakhala mmodzi m'gulu la anthu.<br>Fotokozani kuti nthawi imeneyi Yesu anali mlendo wapadera. Iye ankalowa mu mzinda wa Yerusalemu komaliza chifukwa nthawi inali pafupi yoti akwaniritse cholinga cha Mulungu chofera machimo athu.<br>Mulungu anafuna anthu kuti adziwe kuti Yesu anali munthu wapadera kwambiri. Baibulo limamutcha "Mfumu ya Mafumu ndi Mbuye wa Ambuye". Mulungu anakonzeratu momwe Yesu adzalowere mu Yerusalemu tsiku lopambanali kuti anthu adziwe za Iye.</td></tr>
<tr><td>PHUNZITSANI</td><td>• Pamene Yesu ndi ophunzira ake anayandikira Yerusalemu, Iye anawuza ophunzira ake awiri kuti apite m'mudzi kumene akapeza atamangirira bulu. Iye anawalangiza kuti akamumasule ndi kubwera naye kwa Iye ndipo wina akakafunsa chomwe akuchita iwo akuyankhe kuti, "Ambuye akumufuna." (Luka 19:28-31)<br>• Ganizirani momwe ophunzirawa anapezera bulu ndi kubwera naye kwa Yesu. Kodi kamwana ka bulu kanachita chiyani wina atakwera pa msana pake kwa nthawi yoyamba? Ophunzira anayika zofunda zawo pa msana pake ngati chokhalira ndipo kenaka buluyo analola Yesu akwera pa msana pake. Izi si zimene zinkachitika nthawi zambiri, koma Yesu anali ndi mphamvu pa zolengedwa zonse! (Luka 19:32-35)<br>• Pamene Yesu anayamba kuyenda mu msewumo, anthu ambiri anayamba kuyala zovala zawo mu msewumo. Tsopano anthu anadziwa kuti Iye anali ndani – Mfumu yapadera yotumizidwa ndi Mulungu. Fotokozani kuti mafumu ankakwera pa akavalo pamene akupita ku nkhondo, koma pokwera bulu Yesu anasonyeza kuti Iye wabweretsa mtendere. Anthu anali ndi chisangalalo chachikulu ndipo ankatamanda Mulungu poyimba kuti, "Yodala mfumu imene ikubwera m'dzina la Ambuye." (Luka 19:36-38)<br>• Fotokozani kuti analiponso ena pomwepo amene sankakonda Yesu ndipo anakwiya kuti Iye ankalandiridwa. (Luka 19:39-40) Yesu ankadziwa kuti posachedwa anthu amenewa akwaniritsa zofuna zawo ndipo amupha.<br>• Limbikitsani ana kuti ali ndi chisankho chofunika chomwe akuyenera kuchita chokhudzana ndi Ambuye Yesu. Ife titha kusankha kumulandira m'mitima mwathu kapena kunena kuti "Ayi" kwa Iye ndi kusamupatsa malo. Mulungu akufuna kuti tiyitane Mwana wake m'miyoyo mwathu. Ife tikachita zimenezi tidzalowa m'banja la Mulungu.<br><br>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.<br><br>Onetsani: Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuyang'ana Yesu.</td></tr>
<tr><td>PHUNZIRANI</td><td>Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, Yohane 1:12. Fotokozani kuti mawu akuti landira, vomereza kapena khulupirira ali ndi fundo ya kumulandira munthu. Onetsani kuti mawu akuti "Iye" ana amvetsa kuti ndi ndani.</td></tr>
<tr><td>KUMBUKIRANI</td><td>Lembani zoona/zabodza pa mawu awa.<br>• Yesu ndi ophunzira ake ankalowa mu Yerusalemu.<br>• Yesu anatuma ophunzira ake atatu kupita ku mudzi.<br>• Iwo anakwera bulu.<br>• Bulu sanadandaule pamene Yesu anakwera pa msana pake.<br>• Anthu anayika chopondera pansi.<br>• Aliyense analandira Yesu.<br>• Yesu ndi Mfumu ya Mafumu ndipo akuyenera kulandiridwa.<br>• Pamene tamulandira Yesu m'miyoyo mwathu tikhala a m'banja la Mulungu.</td></tr>
</table>

## B4 Nkhani Yoyamba

**Kufa kwa Yesu – Iyi ndi nkhani ya Ambuye Yesu kutifera ife.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Anamuchita nkhanza Yesu ndipo sankayenera kufa.<br>• Ambuye Yesu anafa kuti atipulumutse ku machimo athu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 23:33***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 23:1-26, 32-43*** |
| **MAWU OYAMBA** | Pangani makadi amene alembedwa kuti: **kukhumudwitsidwa ndi mnzako, kulanga wosalakwa, kusekedwa, kuchitidwa mwano**. Perekani zitsanzo za tsiku ndi tsiku m'magulu momwe ana atha kuyankhula zomwe zinawachitikira ndi momwe anamvera mu mtima mwawo. Ife tikufuna zimenezi zitasiya kuchitika!<br>Fotokozani kuti Ambuye Yesu ankadziwa kuti akuchitidwa nkhanza ndi chiyani. Anthu anachita zonsezi kwa Iye ndiponso zoposa. Lero tiona chifukwa chimene Iye anavutika motere. |
| **PHUNZITSANI** | (Ngati mukuphunzitsa pa sukulu ndi kofunika kulemba mnzere chotsitsa kuti muonetse zomwe zinachitika pophunzitsa. Jambulani pa makadi zithunzi za **anthu akudya, akupemphera m'munda, akugwidwa ndi adani, akufunsidwa ndi Pilato, gulu la anthu okwiya, akupita kukapachikidwa, mitanda itatu, wachifwamba wokhululukidwa** kuti ana akumbukire zonse zimene zinachitika.)<br>• *Funsani mafunso pang'ono kuti mukumbutse ana za kulowa mu Yerusalemu.* Patatha masiku ochepa chabe Yesu anali pa chakudya chamadzulo ndi ophunzira ake, chomaliza asanafe. Kenaka anapita ku munda kukapemphera. *Onetsani zochitika – usiku, kuli zii, kenaka akumva kuyenda kwa anthu ali ndi Yudase kuti adzagwire Yesu. Fotokozani chisoni chimene Yesu anali nacho nthawi imeneyi.* ***(Luka 22:7-20 ndi 22:39-53)***<br>• Tsiku lotsatira, anapita ndi Yesu kwa Pilato, bwanamkubwa. ***(Luka 23:1-4, 20-25)*** *Fotokozani mphamvu za udindo wake ndipo tsindikani kuti sanapeze cholakwa chilichonse pa moyo wa Yesu. Ambuye Yesu anali wangwiro ndi wopanda tchimo.* Pamapeto pake, Pilato anachita zomwe anthu okwiya aja anafuna ndipo anaweruza kuti Yesu aphedwe. *Kwa ife zikuoneka kuti kunali kusowa kwa chilungamo koma mbali ya Mulungu chinali chikonzero chake kuti atipulumutse ife!*<br>• Anapita ndi Yesu kunja kwa Yerusalemu. Munthu wina wotchedwa Simoni anakakamizidwa kunyamula mtanda. ***(Luka 23:26)*** Atafika pa phiri, asilikali anakhomera Yesu pa mtanda. Achifwamba awirinso anaphedwanso nthawi imeneyi, wina mbali ina winanso mbali ina. Pamene Yesu anali pa mtanda asilikali ankamuseka ndiponso mwa achifwambayo anayankhula mawu a mwano. Wachifwamba winayo anazindikira kuti Yesu sanali ngati iwo. Iye anazindikira kuti akufa chifukwa anachita zoyipa koma Yesu palibe choyipa chomwe anachita. Iye anazindikira chomwe Yesu anali ndipo anapempha kuti amukumbukire. Yesu analonjeza kuti tsiku lomwelo, iye adzakhala naye Kumwamba. ***(Luka 23:32-43)***<br>• *Fotokozani kuti monga wachifwamba, tikuyenera kuzindikira kuti Yesu sankayenera kufa. M'malo mwake anasautsidwa ndi kufa ndi cholinga choti aonetsa chikondi chachikulu cha Mulungu polangidwa chifukwa cha machimo athu. Ngati tipempha kuti atikhululukire, ifenso titha kutsimikizika kuti tsiku lina tidzapita Kumwamba.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kufa kwa Yesu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Luka 23:33***, kapena gawo chabe, molingana ndi zomwe ana angathe kuchita. Fotokozani dzina la phiri pamene Yesu anafera. Ndime ina itha kukhala ***1 Petro 3:18***. |
| **KUMBUKIRANI** | Sakanizani makadi ojambulidwa aja ndipo lolani ana ayike molondola. Ngati mukuphunzitsa gulu laling'ono la ana, mukhale ndi zolemba za magulu osiyana kuti amene atsirize msanga ndiye apambane. |

## B4 Nkhani Yachiwiri

**Yesu amwalira ndi kuyikidwa m'manda - Iyi ndi nkhani ya kufa ndi kuyikidwa m'manda kwa Yesu.**

**Ife tikuphunzira kuti:**

- Imfa ya Yesu inali yosiyana ndi imfa zina zonse chifukwa Iye analangidwa chifukwa cha machimo athu.
- Ife tikuyenera kumuthokoza Iye chifukwa cha chikondi chake chachikulu pa ife.

**Vesi Yoloweza:** ***1 Akorinto 15:3-4***
**Ndime Yowerenga:** ***Luka 23:44-56***

### MAWU OYAMBA

Yankhulani za usana ndi usiku, momwe zimachitikira. Ife timayembekezera kuti usiku ubwere mu nthawi yake! Umu ndi mmene Mulungu analengera. Koma tsiku limene Yesu anafa linali losiyana. Mwadzidzidzi, popanda chenjezo, nthawi ya 12 koloko masana, dzuwa linaleka kuwala ndipo kunali mdima ngati usiku. Izi zinachitika kwa maora atatu. ***(Luka 23:44, 45)*** N'chifukwa chiyani Mulungu analola kuti izi zichitike?

### PHUNZITSANI

- Baibulo likutiwuza kuti m'maora atatu amenewa Ambuye Yesu ankalangidwa ndi Mulungu chifukwa cha tchimo lathu. *Funsani ana ngati akumbukira mmene Yesu anavutikira mu nkhani ya sabata latha. Fotokozani kuti tingathe kumvetsa pang'ono momwe Iye anavutikira koma sitingathe kumvetsetsa za chilango cha tchimo lathu. Yesu anazunzika mwa ufulu wake chifukwa cha chikondi chake pa ife ndipo anafuna kukwaniritsa chikonzero cha Atate ake kuti ife tipulumutsidwe.*
- Potsiriza, Yesu anapemphera ndi kupereka mzimu wake kwa Mulungu. ***(Luka 23:46)*** Iyi inali njira ya Yesu yonena kuti watsiriza ntchito yomwe Atate ake anamutuma kudzagwira. *Fotokozani za kukhutitsidwa kumene kumakhalapo tikatsiriza ntchito yosavuta, ndi kudziwa kuti palibe chatsala choti tichitenso – monga: kupanga chinthu. Yesu anachita zonse zimene zinkafunika kuchitika kuti tikhululukidwe tchimo lathu. Limbikitsani ana za kufuna kwa kuvomereza zimene Yesu anachita m'malo mwawo.*
- Kenaka Yesu anafa. *Fotokozani momwe abwenzi ake anamvera m'mitima mwawo.* Bwenzi labwino lotchedwa Yosefe anapita kwa Pilato ndi kukapempha thupi la Yesu. Iye analitsitsa mosamala pa mtanda paja, kulikuta ndi nsalu yoyera ndi kuliyika m'manda atsopano. *Fotokozani kuti manda ake anali ngati phanga laling'ono.* Kenaka anagubuduza mwala ndi kutseka pa khomo pa mandawo. ***(Luka 23:50-53)***

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Yesu amwalira ndi kuyikidwa m'manda.

### PHUNZIRANI

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***1 Akorinto 15:3-4***. Ana aang'ono anene mawu asanu oyambawo. Onetsetsani kuti ana akudziwa Malembawa ndipo fotokozani kuti izi zinachitika kwa Ambuye Yesu monga analembera m'Chipangano Chakale zaka 500 za m'mbuyomo.

### KUMBUKIRANI

Lembani zoona/zabodza pa mawu awa.

- Mdima unayamba nthawi ya masana.
- Unakhala maora anayi.
- Nthawi ya mdima, Yesu analangidwa chifukwa cha tchimo lathu.
- Yesu anayankhula kwa Atate ake asanamwalire.
- Abwenzi a Yesu anamvetsetsa zonse zimene zinamuchitikira.
- Yosefe anapempha asilikali kuti amupatse thupi la Yesu.
- Iye analikulunga m'nsalu yoyera.
- Iye anayika thupilo m'manda.

## B4 Nkhani Yachitatu
**Yesu akhalanso ndi moyo - Iyi ndi nkhani ya Mariya kuzindikira kuti Yesu ali moyo!**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Mulungu anaukitsa Yesu patatha masiku atatu atafa.<br>• Monga Mariya anazindikira kuti Ambuye auka, nafenso tingathe.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Aroma 10:9***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Yohane 20:1-18*** |
| **MAWU OYAMBA** | M'phunziro lathu lapita, tinaphunzira za kufa kwa Yesu pa mtanda. Fotokozani kuti kwa ife iyi ndi nkhani yabwino! Kudzera mu imfa ya Yesu pa mtanda, Mulungu anapereka njira yoti tikhululukidwe machimo athu. Chikonzero chodabwitsa cha Mulungu chinakwaniritsidwa! Koma abwenzi a Yesu anakhumudwa ndipo anali ndi chisoni. Iwo sankamvetsetsa zinthu monga mmene ife tikumvera kudzera m'Baibulo. Koma iwo sanakhala achisoni nthawi yayitali! Nkhani iyi inali ndi mathero abwino kwambiri! |
| **PHUNZITSANI** | • *Kumbutsani ana za kuyikidwa m'manda kwa Yesu komanso za manda otsekedwa ndi mwala waukulu.* Tsopano ndi m'mamawa, tsiku lamulungu, tsiku lachitatu Yesu ali m'manda. Mariya, bwenzi labwino la Yesu anapita kukaona manda. *Fotokozani kudabwa kwake pamene anaona kuti mwala wachotsedwa ndipo m'manda mulibemo kathu.* Mariya anathamanga kupita kumene kunali Petro ndi Yohane kuti akawawuze zomwe waona ku manda. *Yankhulani mawu amene anayankhula.* ***(Yohane 20:1-2)*** *Kodi iwo anamva bwanji mu mtima mwawo chifukwa cha nkhani imeneyi?*<br>• Petro ndi Yohane anasangalala ndi nkhani imeneyi ndipo anathamanga momwe akanathera. Yohane ndiye anayamba kufika ndi kusunzumira m'manda koma Petro atafika, analowamo! M'mandamo munali nsalu zokha zimene anakulunga nazo thupi la Yesu. Kenaka Yohane analowanso. Nthawi yomweyo, Yohane anadziwa zomwe zinachitika. Iye anadziwa kuti Yesu ali moyo! ***(Yohane 20:3-9)***<br>• Koma Mariya anali wodabwa. Iye anatsala m'mundamo Petro ndi Yohane atabwerera kwawo. Iye anayima n'kumalira ndi kumayang'ana m'manda muja. Nthawi iyi, Mariya anadabwanso. *Fotokozani za angelo awiri ndipo fotokozani zomwe anakambirana nawo.* ***(Yohane 20:10-13)***<br>• Mariya anatsala yekha, anatembenuka. Panali munthu amene anayima m'munda muja amene sankamudziwa. *Fotokozani zomwe anakambirana.* Nthawi imeneyo mlendo anatchula dzina lake: "Mariya!" Nthawi yomweyo anazindikira mawuwo. Anali a Ambuye ake, Ambuye Yesu! *Mariya anamva bwanji mu mtima mwake?* Mariya anali ndi chimwemwe chachikulu! Iye waona Ambuye. Ambuye anali ndi moyo! Kachiwiri Mariya ananyamuka kupita komwe kunali ophunzira. *Kodi tsopano akawawuza chiyani?* ***(Yohane 20:14-18)***<br>• *Mulungu anaukitsa Ambuye Yesu kwa akufa. Lero ali ndi moyo. Baibulo limanena kuti ali ndi moyo kwamuyaya! Iye akufuna adzaze miyoyo yathu ndi chimwemwe monga Mariya anali nacho atakumana naye pa manda paja. Limbikitsani ana kufunika koti Ambuye Yesu akhale bwenzi lawo ndi zonse zimene akufuna kuwapatsa – kukhululukidwa, mphamvu ndi chimwemwe.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Yesu akhalanso ndi moyo. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Aroma 10:9***. Fotokozani tanthauzo la "kuvomereza" ndi kuti ena adziwe kuti ife timakhulupirira kuti Yesu ndi Ambuye. Vesi iyi ikutiphunzitsa kuti tikuyenera kukhulupirira kuti Mulungu anaukitsa Yesu kwa akufa kuti atipulumutse ku chilango cha machimo athu. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa ngati njira yobwereza nkhaniyi.<br>• Kodi anayamba kupita ku manda ndi ndani?<br>• Kodi Mariya anaona chiyani za mwala?<br>• Kodi iye anapita kukawuza ndani?<br>• Kodi ndani anayamba kulowa m'manda?<br>• Kodi Yohane anachita chiyani atazindikira kuti m'manda mulibe thupi lija?<br>• Kodi Mariya anaona chiyani m'manda atatsala yekha?<br>• Kodi angelo anafunsa Mariya chiyani?<br>• Kodi ndi ndani anali ndi Mariya m'munda muja?<br>• Kodi iye anazindikira bwanji kuti anali Yesu?<br>• Kodi ndi ndani anaukitsa Yesu? |

## B4 Nkhani Yachinayi

**Kuchoka kwa Yesu ndi kubweranso kwake - Iyi ndi nkhani ya kubweranso kwa Ambuye Yesu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Ambuye Yesu anapita Kumwamba ndipo ali kumeneko lero.<br>• Ife tikuyenera kukonzekera kubweranso kwake.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Machitidwe 1:11***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 24:50-53 ndi Machitidwe 1:4-12*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za kutsanzika ndi kupereka chitsanzo – monga: wachibale amene wakhala nanu ndipo akubwerera kwawo kapena wina m'kalasi amene akuchoka pakati panu. **Kapena** fotokozani zomwe zinakuchitikirani inuyo. Mwina munthuyo analonjeza kuti adzabweranso nthawi ina kapena mudzilumikizana naye. Lonjezo limachititsa kusiyana kukhale kosavuta! |
| **PHUNZITSANI** | • Ophunzira a Yesu anali ndi nthawi yabwino yokhala naye atauka kwa akufa. Tsopano anamvetsa chifukwa chomwe ankayenera kufa. Patatha masabata asanu ndi limodzi, Iye anatenga ophunzira khumi ndi mmodzi kupita nawo ku Phiri la Azitona. Iye anawafotokozera kuti nthawi yakwana tsopano yoti abwerere Kumwamba. Iwo sadzakhala okha chifukwa posachedwa adzawatumizira Mthandizi wapadera wotchedwa Mzimu Woyera. Mwadzidzidzi, Yesu akuyankhula nawo, anasiya nthaka ndi kuchoka. *Taganizani iwo akuyang'ana kumwamba, koma nthawi yomweyo Yesu akuzimirira m'mitambo. Mutha kuona za kuti Yesu anakwera Kumwamba (Kalasi 2). Fotokozani zomwe ankamva mu mtima mwawo –kuthedwa nzeru? chisoni?* ***(Machitidwe 1:8-9)***<br>• Nthawi yomweyo angelo awiri anaonekera ndipo anafunsa ophunzira chifukwa chomwe ayimira ndi kumayang'ana m'mitambo. Kenaka angelowo anawawuza kuti Yesu adzabweranso monga mmene amaonera akuchoka pakati pawo. ***(Machitidwe 1:10-11)*** Ophunzira anadziwa sankayenera kukhala pa phiripo, koma m'malo mwake anapita ku Yerusalemu kuti akalandire Mthandizi amene Yesu analonjeza. Iwo sanali ndi chisoni koma anali wodzaza ndi chimwemwe! ***(Luka 24:52)*** *Lumikizani izi ndi mawu oyamba aja onena za anthu amene akuchoka. Fotokozani kuti iwo anakhulupirira kuti Yesu adzasunga lonjezo lake kwa iwo.*<br>• Ambuye Yesu akanali Kumwamba lero koma amene amamukonda akudikira kubweranso kwake. Ife sitikudziwa kuti ndi liti koma tikudziwa kuti zidzachitika – Iye adzasunga lonjezo lake. *Limbikitsani ana za kukhala okonzekera kubweranso kwake ndi kuonetsetsa kuti akumvetsa za kukonzekera kumeneku – pa kukhulupirira Ambuye Yesu kuti awakhululukire machimo awo.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuchoka kwa Yesu ndi kubweranso kwake. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Machitidwe 1:11***. Iyi ndi vesi yayitali – sankhani gawo la vesiyi yomwe ana angathe kuloweza, monga: "Yesu yemweyu..." (Kalasi 2) kapena mawu a mngelo (amene ali mu Kalasi 1). Kumbutsani ana zomwe zikuchitika pamene pali vesi imeneyi – anayankhula ndani, kwa ndani, liti/kuti kumene ananena. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa ngati njira yobwereza nkhaniyi.<br>• Kodi Yesu anali ndi ophunzira angati pa Phiri la Azitona?<br>• Kodi Yesu anawuza ophunzira ake kuti Iye akupita kuti?<br>• Kodi Iye analonjeza kuti adzalandira chiyani?<br>• Kodi ndi chiyani chinamuphinda kuti asamuone?<br>• Kodi angelo anawawuza iwo uthenga wotani?<br>• Kodi kenaka ophunzira anapita kuti?<br>• Kodi Yesu adzabweranso liti?<br>• Kodi Iye akubwera kwa ndani? |

## B5 Nkhani Yoyamba

**Msamariya wachifundo – Iyi ndi nkhani yokhudza kukonda mnansi wathu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Aneba enieni ndi aliyense amene amaonetsa kukoma mtima kwa munthu wosowa.<br>• Yesu akufuna tikhale achifundo kwa ena.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 10:27***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 10:25-37*** |
| **MAWU OYAMBA** | Kalasi 1: Lolani ana ayankhule za amene ayandikana nawo nyumba kwawo. Kodi oyandikana nyumba amathandizana motani? Mtsogoleri ajambule chithunzi chosavuta ndi kulemba zomwe ana akufotokoza kapena mwana wina amene ali ndi zoyankhula achite ngati sewero kapena alole ena aganizire zomwe akutanthauza.<br>Kalasi 2: Fotokozani kuti nkhani ndi zokondweretsa ndipo zitha kukhala zosangalatsa kumvetsera. Funsani ana nkhani zomwe amazikonda kwambiri. Fotokozani kuti Yesu ankayankhula nkhani kuti athandize anthu kumvetsa za Mulungu ndi zomwe akuyenera kuchita. Nkhani zimenezi zimatchedwa **mafanizo**. Tsiku lina munthu wina ankayankhula ndi Yesu. Iye ankadziwa kuti Lamulo la Mulungu limanena kuti, “Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi mphamvu yako yonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mnansi wako monga iwe mwini.” ***(Luka 10:25-28)*** Funsani ana ngati akudziwa tanthauzo la gawo loyamba. Munthuyu sankamvetsa kuti mnansi wake (kapena aneba ake) ndi ndani choncho Yesu anayankhula fanizo ili kuti limuthandize kumvetsa. |
| **PHUNZITSANI** | • Munthu anali paulendo kuchoka ku Yerusalemu kupita ku Yeriko. *Fotokozani kuti uwu unali msewu woopsa, wa ziphompho ndi wokhotakhota ndiponso nthawi zambiri munali anthu achifwamba. Yankhulani ngati sewero kuti mwadzidzi munthuyo anagwidwa ndi kumenyedwa, kuberedwa ndipo anamusiya m’mbali mwa msewu kuti afe. Ngati nthawi ilipo mutha kukambirana kuti izi zikanachitika lero, akanatani.* ***(Luka 10:29-30)***<br>• Pasanatha nthawi, munthu wina anafika ndi kuona zomwe zinachitika koma sanathandize wovulazidwayo! Kenakanso, munthu winanso anafika pamenepo. Anthu onse awiriwa anamulambalala munthuyo. Chomvetsa chisoni kwambiri chinali chakuti anthu onse awiri anali otumikira m’Nyumba ya Mulungu. ***(Luka 10:31-32)***<br>• Munthu wachitatu anafika amene ankachokera dziko lina. *Kwa Kalasi 2 mukuyenera kufotokoza kuti anali Msamariya ndipo Amsamariya ndi Ayuda (munthu wovulazidwayo) sankagwirizana. Simungayembekezera Myuda ndi Msamariya kuthandizana!* Koma Msamariya anayima. Anamupatsa chithandizo choyamba, ndi kumukweza munthuyo pa bulu wake ndi kupita naye ku nyumba ya alendo kumene anapitiriza kumuthandiza usiku umenewo. *Fotokozani momwe anaperekera nthawi yake ndi ndalama zake ndi kuonetsa kuti munthuyo wachira.* ***(Luka 10:33-35)***<br>• Pamene Yesu anatsiriza kufotokoza nkhani imeneyi anafunsa kuti ndi ndani wa anthu atatu amenewa anali mnansi wa munthuyo. *Funsani ana mmene iwo akanayankhira ndipo tsimikizani kuti munthuyo anayankha molondola.* Kenaka Yesu anamuwuza kuti apite akachite zimenezo. *Thandizani ana a Kalasi I kuti amvetse za kuti mnansi ndi ndani … osati yekha amene ayandikana naye nyumba! Afunseni aganizire njira zomwe angaonetse kukoma mtima kwa ena m’kalasimo ndi pabwalo.*<br>• *Ana a Kalasi 2 aganizire za nthawi imene kuonetsa kukoma mtima kwa anthu kutha kukhala kovuta ndi kuti Yesu akutiphunzitsa ife kukhala okoma mtima kwa munthu aliyense, osati kwa okhawo amene ndi abwino kwa ife. Iwo aganizirenso njira zomwe Ambuye Yesu ali ngati Msamariya wachifundo. (Mpulumutsi, Mthandizi ndi Bwenzi)*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Msamariya wachifundo. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n’kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Luka 10:27***. Ana a Kalasi 1 aphunzire gawo lomaliza la vesi. |
| **KUMBUKIRANI** | Kodi nkhani zimene Yesu ankayankhula zimatchedwa chiyani?<br>Kodi munthu ameneyu ankapita kuti?<br>Kodi chinamuchitikira ndi chiyani?<br>Kodi ndi anthu angati amene anadutsa osamuthandiza?<br>Kodi ndi ndani munthu amene anayima?<br>Kodi iye anachita chiyani?<br>Kodi anapereka ndalama zingati kwa woyang’anira nyumba ya alendo?<br>Kodi Yesu anamuwuza chiyani munthuyo kumapeto kwa nkhaniyi? |

## B5 Nkhani Yachiwiri

**Nkhosa yotayika – Iyi ndi nkhani ya momwe Yesu amatisamalira.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Ife tili monga nkhosa yotayika chifukwa timachita zofuna zathu osati zofuna za Mulungu.<br>• Ambuye Yesu ndi M'busa wabwino amene akufuna kutipeza ife.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 10:11***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 15:1-7*** |
| **MAWU OYAMBA** | Kambiranani – Kodi munasocherapo? Kodi chinachitika ndi chiyani? Kodi munamva bwanji? Nanga anakupezani ndi ndani? Kodi munamva bwanji pamene munapezeka?<br>Fotokozerani ana kuti nkhani ya lero ndi m'busa amena nkhosa yake inatayika.<br>Funsani ana zomwe akuganiza kuti m'busa akuyenera kuchita poyang'anira nkhosa zake (kudyetsa, kuteteza, kusamalira ndi zina).<br>Fotokozani kwa ana kuti nthawi zambiri nkhosa zimakonda kuchoka pamene zikuyenera kukhala ndi kutayika. |
| **PHUNZITSANI** | • Tsiku lina amisonkho ena ndi ochimwa anabwera kudzamva zoyankhula za Yesu. Anthu ena anayamba kung'ung'udza ndi kudandaula chifukwa Yesu ankalandira ochimwa. Iye sanasangalale ndi kung'ung'udza kwawo ndipo anayamba kuwawuza nkhani iyi. ***(Luka 15:1-3)*** *Fotokozerani ana kuti Yesu akufuna aliyense abwere kwa Iye. Sizikutengera kuti anthu ndi otani kapena zolakwa zomwe iwo achita.*<br>• Iye anafotokoza nkhani ya m'busa amene anali ndi nkhosa 100. Tsiku lina imodzi inatayika. M'busa anasiya nkhosa zina zija ndi kupita kukafuna yotayikayo. *Tchulani malo ena amene iye anapita kukayifuna. Tsindikani kulimbika kwake. Iye sanali wokondwa mpaka atayipeza.* ***(Luka 15:4)***<br>*Fotokozerani ana kuti Baibulo limanena kuti ife tili ngati nkhosa yotayika. Ambuye Yesu ndi M'busa Wabwino ndipo akufuna atipeze ndi kutisamalira. Funsani ana anene njira zimene Yesu amaonetsera chisamaliro chake pa ife. Muzilembe ndi kulimbikitsa ana kuti ayamike chisamaliro chake. (Onetsetsa kuti mwatsindika kuti njira imene Iye anaonetsera chisamaliro chake ndi kupereka moyo wake chifukwa cha ife.)*<br>• Pamene anayipeza nkhosa ija anasangalala kwambiri. Iye anayinyamula, ndi kuyiyika pa phewa lake kupita nayo ku nyumba. Pamene anafika kwawo, anayitana abwenzi ake ndi anansi kukondwerera chifukwa anayipeza nkhosa yomwe inatayika ija. ***(Luka 15: 5-6)*** *Fotokozerani ana kuti monga munthu uja anali wosangalala atapeza nkhosa yake yotayika, Kumwamba kumakhala chimwemwe chachikulu pamene ife tavomereza zolakwa zathu ndi kukhulupirira Yesu. Kwa ana aang'ono, mufotokoze nkhaniyi moponyerana nawo: kuwerenga, ngati amadziwa manambala awerenge mpaka 99, zochita za m'busa, kukwera, kufunafuna, kupeza ndi kukondwerera.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Nkhosa yotayika. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Yohane 10:11.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani.<br>• N'chifuka chiyani anthu ena sanali okondwa?<br>• Kodi m'busa anali ndi nkhosa zingati?<br>• Kodi ndi zingati zomwe zinasowa?<br>• Kodi m'busa anachita chiyani pamene anazindikira kuti ina yasowa?<br>• Kodi ananyamula motani nkhosa pamene ankapita nayo kwawo?<br>• Kodi anachita chiyani atafika kwawo?<br>• Kodi ndi ndani amene ali ngati nkhosa?<br>• Kodi ndi ndani ali ngati m'busa? |

## B5 Nkhani Yachitatu

**Mwana wolowerera – Iyi ndi nkhani ya kuvomereza tikachita zolakwika.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Mulungu akufuna kuti ife timve chisoni chifukwa cha zinthu zolakwa zomwe tachita.<br>• Mulungu adzatikhululukira pamene tidzavomereza kulakwa kwathu kwa Iye.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 15:24***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 15:11-24*** |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokozerani ana nkhani yayifupi kufuna kuonetsa khalidwe la kukhululukira, monga: *Tsiku lina Yankho ndi Gibo ankasewera pamodzi. Yankho anayamba kusewera ndi mpira umene Gibo ankafuna azisewera nawo. Yankho anakwiya. Iye analanda mpira m'manja mwa Yankho ndi kumugwetsa pansi.*<br>Kambiranani – N'chifuka chiyani Yankho akulira? Kodi mukuganiza kuti Gibo achite chiyani? Kodi mukuganiza kuti Yankho amukhululukire Gibo?<br>Fotokozerani ana kuti nkhani ya lero ya m'Baibulo ndi ya kukhululuka. |
| **PHUNZITSANI** | • Yesu anayankhulanso fanizo lina. Panali munthu amene anali ndi ana awiri aamuna. Mwana wamng'ono tsiku lina anapempha abambo ake kuti amupatse ndalama zomwe zidzakhala zake tsiku lina. Abambo ake anamupatsa ndalama zake. *Kambiranani zomwe mwana ndi abambo ake ankamva m'mitima mwawo.* ***(Luka 15:11-12)***<br>• Pasanapite nthawi yayitali, mwana uja ananyamula katundu wake ndi kupita ku dziko lakutali. Iye ali kumene analiko, anaononga ndalama zake pochita zoyipa. Munagwa njala m'dzikomo. *Fotokozani kuti njala ndi chiyani. Kambiranani momwe anadziwira kuti ndalama zake zonse zatha, ndi vuto limene anali nalo. Kambiranani - Kodi mukuganiza mwanayo anamva chiyani mu mtima mwake pamene anazindikira kuti alibe chilichonse? Kodi mukuganiza kuti akanachita chiyani?*<br>• Mnyamata analibe munthu amene akanapita kuti apemphe thandizo. Iye anapeza ntchito yoweta nkhumba. Nthawi zina ankakhala ndi njala mpaka kufuna kudya chakudya cha nkhumbazo. ***(Luka 15:13-16)***<br>• Tsiku lina anayamba kuganizira kwawo. *Thandizani ana kuti amvetse kuti mnyamatayu ankaoneka motani pa ulendo wake wobwerera kwawo. Siyanitsani ndi ulendo wake wochoka kwawo.* Iye anazindikira kuti antchito akwawo anali ndi chakudya chokwanira. Iye anachita chiganizo chobwerera kwawo kwa abambo ake, ndi kukawawuza kuti analakwitsa ndiponso kuwapempha kuti akhale wantchito wawo. Abambo ake anamuona akubwera patali. Abambo ake anathamanga kukakumana naye ndi kumupsopsona. Fotokozani za kudabwa kwake pamene abambo ankabwera akuthamanga kwa iye. Mwana anayamba kuyankhula kuti analakwitsa, koma abambo ake anamudula mawu. Iye anawuza antchito ake kuti akatenge mkanjo wabwino, mphete ndi nsapato kuti adzamuveke. Abambo anakonza phwando lalikulu chifukwa cha kubwerera kwa mwana wawo. ***(Luka 15:20-24)*** *Funsani ana afotokoze zomwe abambo ankachita kwa mwana wawo (monga: kukoma mtima, kukhululuka ndi kusangalala kwambiri).*<br>• *Kambiranani – Kodi mukuganiza kuti mwana anamva bwanji mu mtima mwake pamene anabwerera kwawo? Fotokozerani ana kuti ifenso tili ngati mwanayu chifukwa tachita zolakwa zambiri. Mulungu ndi Atate a Akhristu. Iye akufuna ife kuti tipite kwa Iye ndi kumuwuza kuti ndife olakwa. Kambiranani – Kodi inu munayamba mwavomereza kulakwa kwanu kwa munthu wina koma iye sanamve kapena kukukhululuka? Uzani ana kuti Mulungu NTHAWI ZONSE amamvetsera ndi kutikhululukira pamene tamuwuza za kulakwa kwathu.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Mwana wolowerera. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Luka 15:24***. Fotokozani kuti abambo sankadziwa zomwe zinamuchitikira mwana wawo - anali ngati wakufa kwa iwo. Koma tsopano wabwerera, ali bwino komanso ali moyo! |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani.<br>• Kodi abambowa anali ndi ana angati?<br>• Kodi mwana wamng'ono anapempha chiyani kwa abambo ake?<br>• Kodi mwana anachita chiyani ndi ndalama zake?<br>• Kodi anapeza ntchito yotani?<br>• Kodi kenaka anaganiza zochita chiyani?<br>• Kodi abambo ake anachita chiyani pamene anamuona akubwerera kwawo?<br>• Kodi abambo anampatsa mwana wawo chiyani?<br>• Kodi abambo ali ngati ndani m'nkhaniyi? |

**B5 Nkhani Yachinayi**

**Wofesa mbewu – Iyi ndi nkhani ya momwe timamvera Mawu a Mulungu.**

**Ife tikuphunzira kuti:**

- Baibulo ndi Mawu a Mulungu.
- Mulungu akufuna kuti tikhale ngati nthaka yabwino ndi kukhulupirira zimene akunena m'Baibulo.

**Vesi Yoloweza:** ***Marko 4:20***

**Ndime Yowerenga:** ***Marko 4:1-20***

**MAWU OYAMBA**

Kambiranani – Kodi munayesapo kudzala mbewu? Kodi munadzala chiyani? Kodi mbewu inkafuna chiyani kuti ikule? Kodi inakula ndi kukhala yabwino kapena inafa? Kapena ndi gulu laling'ono mutha kuonetsa mbewu zosiyanasiyana kapena zomera.
Fotokozani kwa ana kuti nkhani ya lero ndi ya mlimi amene akufuna kudzala mbewu.

**PHUNZITSANI**

- Anthu ambiri anabwera kudzamva Yesu akuyankhula. Panali anthu ambiri motero Yesu analowa m'bwato ndi kukhala m'nyanja pamene ankaphunzitsa anthu amene anali pa mtunda. ***(Marko 4:1-2)*** *Kambiranani – kodi mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani aliyense ankafuna kumva nkhani zomwe Yesu ankayankhula? Kodi mukuganiza kuti inunso mukanafuna kumvetsera nkhani zake ngati mukanakhalapo nthawi imeneyo?*
- Panali mlimi amene anafesa mbewu zake pa nthaka. Mbewu zinagwera pa nthaka zosiyanasiyana. Zina zinagwera m'mbali mwa njira ndipo mbalame zinatola ndi kudya, choncho sizinamere. Zina zinagwera pa nthaka ya miyala. Zinalephera kuzika mizu, motero mosachedwa zinafa. Zinanso zinagwera pa minga ndipo mingazo zinalepheretsa kuti zikule. Panali mbewu zina zomwe zinagwera pa nthaka yabwino. Panali zomera zabwino. ***(Marko 4:3-9)*** *Fotokozerani ana kuti mbewu mu nkhani iyi ili ngati Mawu a Mulungu. Baibulo ndiye Mawu a Mulungu. Fotokozani kuti ngati mukufuna kumva Mawu a Mulungu muziwerenga Baibulo.*
- Yesu anapitiriza kumasulira fanizoli. Pamene mbewu zomwe zinagwa m'mbali mwa njira ndipo mbalame zinazidya ndi anthu amene amamva Mawu a Mulungu ndipo Satana amabwera ndi kuwalanda. Pamene mbewu zinagwa pa miyala ndi anthu amene amamva Mawu a Mulungu nayamba kutsatira Yesu koma kenaka amasintha maganizo awo chifukwa cha zovuta zomwe akukumana nazo. Pamene mbewu zinatchingika ndi minga ndi anthu amene amamva Mawu a Mulungu, koma amaganiza kwambiri za ndalama zawo ndi chuma chawo kuposa za Ambuye Yesu. Pamene mbewu zinagwa pa nthaka yabwino ndi anthu amene amamva Mawu a Mulungu ndi kuwalandira ndipo amakula ndi kukhala Akhristu amphamvu. ***(Marko 4:13-20)*** *Fotokozani kuti Mulungu akufuna kuti tikhale nthaka yabwino ndi kukhulupirira zomwe Iye akunena m'Mawu ake Baibulo. Kambiranani – kodi tingakhale bwanji nthaka yabwino?*
- *Kambiranani – Kodi ndi fanizo liti mwa amene taphunzira lomwe ndi labwino kwambiri kwa inu? N'chifukwa chiyani mukulikonda? Kodi ndi phunziro lofunika lotani limene mwalipeza m'fanizoli?*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Wofesa mbewu.
Onetsani mbewu zina, monga chimanga, ndiponso yankhulani za chimanga chomwe atsala pang'ono kukolola. Izi zidzathandiza kupereka chitsanzo cha kuchuluka kwa mbewu zomwe zatchulidwa mu Vesi Yoloweza. Mutha kusankha kugwiritsa ntchito mu Kalasi 1 - ***Salimo 119:42*** monga m'phunziro la Nthawiyabaibulo.

**PHUNZIRANI**

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Marko 4:20***. Muchite zizindikiro zomwe zithandize ana kukumbukira chilichonse mu nkhaniyi monga, kufesa = kuwaza, kumva = kuomba m'manja, kulandira = kuloza pa mtima, kubereka = kugwirana manja ndi kukweza m'mwamba. Mulembe kuchuluka kwake m'malere.

**KUMBUKIRANI**

Funsani ana mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani.

- Kodi Yesu anali kuti pamene ankaphunzitsa anthu?
- Kodi mlimi anachita chiyani?
- Kodi malo oyamba pamene panagwera mbewu panali pati?
- Nanga malo achiwiri inali nthaka yotani?
- Nanga nthaka yachitatu inali yotani?
- Nanga nthaka yachinayi inali yotani?
- Kodi ndi nthaka iti yomwe inali yabwino kwambiri yoti mbewu zinamera?
- Kodi mbewu ili ngati chiyani?

## B6 Nkhani Yoyamba

**Mnyamata wa maloto – Iyi ndi nkhani ya banja la Yosefe ndi maloto ake achilendo.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Moyo wa m’banja la Yosefe sunali wosangalala nthawi zonse.<br>• Mulungu anali ndi cholinga ndi moyo wa Yosefe ndiponso Iye ali ndi cholinga ndi miyoyo yathunso.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Genesis 37:8***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Genesis 37:1-11*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yosefe anali ndi achimwene ake khumi ndi mmodzi. Funsani ana atchule mayina a achimwene ndi alongo awo. Kodi inu muli nawo angati? Kodi mumaona bwanji kukhala woyamba/wapakati/wamng’ono kwambiri m’banja mwanu? Kambiranani zikanakhala zotani mukanakulira m’banja la ana ambiri ngati limeneli. |
| **PHUNZITSANI** | • Yakobo, abambo a Yosefe, ankakhala m’dziko la Kanani. Yosefe anali ndi zaka 17. Iye ankathandiza achimwene ake kuyang’anira ziweto za abambo ake. Tsiku lina anawaona akuchita chinthu cholakwika. Iye anawuza abambo ake nkhaniyi. ***(Genesis 37:1-2)***<br>• Yakobo ankakonda kwambiri Yosefe kuposa ana enawo chifukwa anali mwana wobwadwa iye atakalamba. Yakobo anapangira Yosefe mkanjo wokongola wa mitundu yambiri yosiyanasiyana. Pamene achimwene ake a Yosefe anaona anamuchitira nsanje kwambiri. Iwo anamuda! ***(Genesis 37:3-4)*** *Kambiranani mawu akuti ‘nsanje’ ndi ana. Kodi kukhala ndi nsanje zikutanthauza chiyani? Kodi inu munachitapo nsanje? Kodi mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani achimwene a Yosefe anali ndi nsanje?*<br>• Yosefe anali ndi maloto. Analota iye pamodzi ndi achimwene ake akugwira ntchito m’munda yomanga mitolo ya tirigu. Mtolo wa Yosefe unayimirira ndipo mitolo ya achimwene ake inabwera ndi kudzagwadira mtolo wake.<br>• *Fotokozerani ana kuti maloto awa anali ndi tanthauzo lapadera kwa Yosefe la zomwe zidzamuchitika mtsogolo. Funsani ana akambirane zomwe akuganiza kuti ndi tanthauzo la malotowo.* Abale ake anamuda kwambiri chifukwa cha maloto ake amene anawafotokozera. ***(Genesis 37:5-8)***<br>• Yosefe anali ndi maloto enanso ofanana tanthauzo ndi oyamba aja. Nthawi iyi anaona dzuwa, mwezi ndi nyenyezi khumi ndi imodzi zikumugwadira. Tsopano ngakhalenso abambo ake anakwiya naye. Iwo anati, “Kodi uganiza kuti ine, amayi ako pamodzi ndi abale ako onsewa tingadzabwere kudzakugwadira iwe?” ***(Genesis 37:9-10)***<br>• Abale ake a Yosefe anachita naye nsanje kwambiri koma abambo ake ankaganizira za tanthauzo la malotowa. ***(Genesis 37:11)****. Funsani ana afotokoze zomwe akuganiza kuti zidzamuchitikira Yosefe mtsogolo. (Maloto ankatanthauza kuti tsiku lina iye adzalamulira achimweme ake.) Kumbutsani ana kuti Mulungu anali ndi cholinga ndi moyo wa Yosefe kuyambira pachiyambi. Mulungu ali ndi cholinga ndi miyoyo yathunso.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Mnyamata wa maloto. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n’kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Genesis 37:8***. Mwina mbali yoyamba yokha kwa ana aang’ono kwambiri. Fotokozani kuti achimwene a Yosefe ankamvetsa tanthauzo la maloto ake. Iwo ankachita naye nsanje ndi kudana naye. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani.<br>• Kodi m’nkhaniyi Yosefe anali ndi zaka zingati?<br>• Kodi Yakobo anapereka mphatso yotani kwa Yosefe?<br>• N’chifukwa chiyani achimwene a Yosefe ankamuchitira nsanje?<br>• Kodi nsanje ndi chiyani?<br>• Kodi mukuganiza kuti ndi bwino kukhala ndi nsanje? (yankhani inde kapena ayi)<br>• Kodi Yosefe analota chiyani m’maloto woyamba ndi achiwiri?<br>• Kodi maloto a Yosefe ankatanthauza chiyani?<br>• Kodi ndi ndani anali ndi cholinga ndi moyo wa Yosefe kuchokera pachiyambi?<br>Ngati njira ina, ana apange chinthu chooneka ngati mkanjo wa Yosefe. Iwo ajambule pa pepala ndi kulidula zigawo khumi ndi ziwiri. Gulu lililonse laling’ono likhale ndi gawo limodzi la pepalalo koma la mtundu umodzinso. Mkanjowo magawo awabweretse pamodzi akatsiriza kuti apangenso mkanjo uja. |

## B6 Nkhani Yachiwiri

**M'bale wosakondedwa – Iyi ndi nkhani ya Yosefe kugulitsidwa ndi abale ake.**

**Ife tikuphunzira kuti:**

- Yosefe anagulitsidwa ndi abale ake ku ukapolo.
- Sitingathe kubisa machimo athu pamaso pa Mulungu.

**Vesi Yoloweza:** ***Numeri 32:23***
**Ndime Yowerenga:** ***Genesis 37:12-36***

### MAWU OYAMBA

Funsani ana ngati amagwira ntchito yomwe makolo awo amawapatsa ndi kupita komwe awatuma monga Yosefe ankachitira. Kumbutsani ana nkhani imene tayiona kale m'mbuyo. N'chifukwa chiyani abale ake sankakonda Yosefe? M'nkhani ya lero, Yosefe anatumidwa ndi abambo ake kuti apite akaone abale ake omwe anali kutali ndi kwawo kuweta nkhosa zawo. ***(Genesis 37:12-17)***

### PHUNZITSANI

- Abalewo anaona Yosefe akubwera. Iwo ankamuda kwambiri ndipo anagwirizana zomupha. Kodi chikanachitika ndi chiyani ndi maloto ake aja? Iwo anakonza zoti akanamize abambo awo kuti anaphedwa ndi chirombo. ***(Genesis 37:18-20)*** *Fotokozani kuti abalewo ankaganiza kuti akanatha kubisa machimo awo ndipo palibe amene akanazindikira zomwe anachita. Mulungu amadziwa zolakwa zonse zimene ife timachita.*
- Rubeni, m'bale wamkulu wa Yosefe, anawaletsa zochita zimenezi. M'malo mwake anawawuza kuti amuponye Yosefe m'dzenje. Iye anakonza zoti abwerenso nthawi ina kudzamupulumutsa. ***(Genesis 37:21-22)***
- Pamene Yosefe anafika, anamuvula mkanjo wake wamitundu yosiyanasiyana uja ndi kumuponyera m'dzenje lopanda kanthu. ***(Genesis 37:23-24)***
- Pasanapite nthawi, anthu ena ankadutsa. Iwo ankapita kukagulitsa zokometsera zakudya ku Aigupto kukagulitsa. Mmodzi mwa abale ake, Yuda, ankafuna kukhala ndi ndalama. M'malo momupha Yosefe, iye anapereka maganizo akuti amugulitse kwa anthu amenewo. Iwo anamugulitsa Yosefe pa mtengo wa ndalama zasiliva makumi awiri. Anapita ndi Yosefe ku Aigupto kuti akagwire ntchito ngati kapolo. ***(Genesis 37:25-28)*** *Kodi kapolo ndi ndani? Kodi mukuganiza kuti nthawi imeneyi Yosefe ankamva bwanji mu mtima mwake?*
- Abale ake anayesetsa kubisa zomwe anachita. Iwo anatenga mkanjo wokongola uja wa Yosefe ndi kuunyika m'magazi a mbuzi. Iwo anautenga ndi kupita nawo kwa abambo awo ndi kuwafunsa ngati unali wa Yosefe. Yakobo anauzindikira mkanjowo. Iye anaganiza kuti chirombo cholusa chinamupha Yosefe. Yakobo anamva chisoni kwambiri ndipo sankanatonthozeka. ***(Genesis 37:29-35)***
- Nthawi imeneyi, Yosefa anali ndi moyo ku Aigupto. Iye anagulitsidwa kwa munthu wotchedwa Potifara amene anali mkulu wa ankhondo a Farao. ***(Genesis 37:36)***
- *Kumbutsani ana ngakhale zinthu zinali zovuta kwambiri kwa Yosefe, Mulungu ndiye ankalamulira zonse zomuchitikira.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – M'bale wosakondedwa.

### PHUNZIRANI

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Numeri 32:23***. Onetsetsani kuti ana akumvetsa tanthauzo la 'tchimo' ndi kuti akuyenera kulangidwa. Fotokozani kuti Mulungu amadziwa machimo athu onse ndipo machimo akuyenera kulangidwa. Kumbutsani ana kuti Ambuye Yesu anafa pa mtanda kuti achotse chilango cha machimo athu.

### KUMBUKIRANI

Funsani ana mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani.

- Kodi Yakobo anawuza Yosefe kuti achite chiyani kumayambiriro kwa nkhani yathu lero?
- Kodi abale anakonzekera kuchita chiyani kwa Yosefe?
- Kodi ndi m'bale uti amene anawawuza kuti asamuphe Yosefe koma amuponye m'dzenje?
- Kodi anagulitsa Yosefe ndi ndalama zingati zasiliva?
- Kodi abale ake anachita chiyani pofuna kubisa tchimo lawo?
- Kodi Yakobo anaganiza kuti chinachitika ndi chiyani kwa Yosefe?
- Kodi ndi ndani amene ankaona zonse zimene zinkachitika pa moyo wa Yosefe?
- Kodi Vesi Yoloweza ikuchokera m'buku lanji?

## B6 Nkhani Yachitatu

## Kapolo wabwino – Iyi ndi nkhani ya Yosefe kuponyedwa m'ndende.

**Ife tikuphunzira kuti:**

- Yosefe anali woona mtima ndi wolimbikira ntchito ngakhale ali m'ndende.
- Mulungu anali ndi Yosefe ndipo sadzatisiya ife kapena kutikhumudwitsa.

**Vesi Yoloweza:** ***Genesis 39:2***

**Ndime Yowerenga:** ***Genesis 39:1-6 ndi 19-23***

**MAWU OYAMBA**

Funsani ana ngati anakhalapo kutali ndi abale awo. Kodi iwo ankamva bwanji mu mtima mwawo? Mwachidule kumbutsani ana momwe Yosefe amapezekera kuti ali kutali ndi abale ake ndi momwe anapezekera kwa Potifara ngati kapolo. Fufuzani kuti muone mwina zomwe Yosefe anachita nthawi imeneyi pamene anafika ku dziko lachilendo ndi kugulitsidwa ngati kapolo.

**PHUNZITSANI**

- Anapita ndi Yosefe ku Aigupto ndipo anamugulitsa ngati kapolo kwa Potifara. Potifara anali mkulu wa ankhondo a mfumu. Potifara anaona kuti Yosefe anali munthu woona mtima ndi wogwira ntchito molimbika. Iye anazindikira kuti Mulungu anali ndi Yosefe ndipo anamuyika kukhala woyang'anira nyumba yake. ***(Genesis 39:1-4)***
- Kuyambira pamene Potifara anayika Yosefe kukhala wolamulira nyumba yake, Mulungu anadalitsa nyumba ya Potifara. Yosefe anali wodalirika moti Potifara anasiya zonse m'manja mwake kuti azichita ziganizo. ***(Genesis 39:5-6)*** *Thandizani ana kuti amvetsetse za madalitso pofotokoza kuti kukoma mtima kwa Mulungu kunali pa nyumba ya Potifara chifukwa cha Yosefe. Kumbutsani ana kuti Mulungu anali ndi Yosefe ndipo ankamuyang'anira.*
- Tsiku lina, mkazi wa Potifara anamunamizira Yosefe chinthu chimene sanachite. Iye ananena zabodza kwa Potifara. Potifara anakhulupirira mkazi wake. Iye anakwiya kwambiri ndipo anaponya Yosefe m'ndende ngakhale sanalakwe chilichonse. ***(Genesis 39:19-20)*** *Fotokozani kusintha kwakukulu komwe kunachitika, kuchoka m'nyumba ya Potifara ndi kupita ku ndende. Kodi Mulungu anali atamuyiwala Yosefe? Kodi inu ena anakunenerani zoyipa zomwe simunachite? Kodi munamva bwanji mu mtima mwanu?*
- Koma Mulungu anali ndi Yosefe ndi kumusamalira ngakhale anali m'ndende. Yosefe anapitiriza kukhala woona mtima ndi wolimbikira ntchito. Woyang'anira ndende anayika Yosefe kuti akhale woyang'anira andende anzake. Chilichonse chimene Yosefe ankachita m'ndende, Mulungu ankadalitsa. ***(Genesis 39:21-23)***
- *Fotokozani mwachidule makhalidwe abwino amene Yosefe anaonetsa mu nkhani imeneyi. Kukanakhala kosavuta kwa Yosefe kusiya Mulungu koma Yosefe anapitiriza kukondweretsa Mulungu. Mulungu ankamukonza Yosefe kuti adzakhale pa udindo wina m'tsogolo. Mulungu sanayiwale Yosefe ndipo Iye sakanamukhumudwitsa.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Onetsani:** Onani FBI Zoonjezera C – Kapolo wabwino.

**PHUNZIRANI**

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***Genesis 39:2 (gawo a)***. Fotokozani kwa ana kuti nthawi zina cholinga cha Mulungu pa ife ndi kudutsa nthawi zovuta. Koma, Mulungu amatikonda ndipo amakhala nafe nthawi zonse.

**KUMBUKIRANI**

Funsani ana mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani.

- Kodi Yosefe anapita naye ku dziko lanji?
- Kodi ndi ndani amene anagula Yosefe?
- Kodi Potifara ankagwira ntchito yotani?
- N'chifukwa chiyani Potifara anayika Yosefe kukhala woyang'anira nyumba yake?
- N'chifukwa chiyani Yosefe anayikidwa m'ndende?
- Kodi Yosefe anachita cholakwa chilichonse?
- Kodi ndi ndani amene anali ndi Yosefe, kuti zonse zidzimuyendera bwino?
- N'chifukwa chiyani Mulungu analola kuti Yosefe aponyedwe m'ndende?

## B6 Nkhani Yachinayi

**Mtsogoleri watsopano – Iyi ndi nkhani ya Yosefe kumasulira maloto a Farao.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yosefe anakhala wachiwiri kwa wolamulira m'dziko la Aigupto.<br>• Mulungu anakonza Yosefe kuti athe kugwira ntchito yapadera.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Akorinto 10:13***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Genesis 41:14-49*** |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ngati anadzuka atalota maloto woyipa. Kodi iwo anamva bwanji mu mtima mwawo? Mu nkhani iyi, Farao, Mfumu ya Aigupto inali ndi maloto awiri amene sankawamvetsa. Iye ankafuna kudziwa matanthauzo ake! Kodi ndani amene akanamuthandiza? |
| **PHUNZITSANI** | • Farao ankafuna kudziwa matanthauzo a maloto awiri amenewa. M'maloto ake woyamba, iye analota ng'ombe zisanu ndi ziwiri zonenepa zikutuluka mu Mtsinje wa Nailo. Kenaka munatulukanso ng'ombe zina zisanu ndi ziwiri zoonda. Ng'ombe zoonda zinadya zonenepa zija koma zinakhalabe zoonda ngati poyamba! Kenaka analotanso ngala za tirigu zisanu ndi ziwiri zabwino kwambiri ndi ngala zina zisanu ndi ziwiri zowauka. Ngala zowauka zinameza ngala zabwino zija. Farao anafunsa anthu amatsenga kuti amasulire malotowo koma analephera. ***(Genesis 41:1-8)***<br>• *Funsani ana kuti akuwuze zomwe akuganiza kuti ndi tanthauzo lake. Mulungu ndiye analotetsa Farao maloto amenewa. Ndi Mulungu yekha amene akanapereka tanthauzo lake.*<br>• Farao anayitanitsa Yosefe. Yosefe anatulutsidwa m'ndende ndi kubwera pamaso pa Farao. *Funsani ana kuti aganize kuti izi zinkatanthauza chiyani kwa Yosefe - kambiranani za kusiyana kwa m'ndende ndi nyumba yaufumu.* Iye anawuza Farao kuti sangathe kutanthauzira pa yekha koma Mulungu ndiye angamuthandize kumasulira malotowo. ***(Genesis 41:14-24)*** *Thandizani ana kuti amvetse za kudalira Mulungu kwa Yosefe.*<br>• Mulungu anawuza Yosefe tanthauzo la malotowo. Yosefe anawuza Farao tanthauzo lake. Ng'ombe zisanu ndi ziwiri zonenepa ndi ngala za tirigu zisanu ndi ziwiri zabwino ndi zaka zisanu ndi ziwiri za zokolola zabwino. Aliyense adzakhala ndi chakudya chambiri. Koma, ng'mbe zisanu ndi ziwiri zoonda ndi ngala za tirigu zisanu ndi ziwiri zowauka zikutanthauza pambuyo pa zaka zisanu ndi ziwiri zakudya zambiri padzakhala zaka zisanu ndi ziwiri za njala. Njala yake idzakhala yoyipa kwambiri mpaka aliyense adzayiwala za zaka zisanu ziwiri za chakudya chambiri zija. ***(Genesis 41:25-32)*** *Fotokozani tanthauzo la njala, perekani chitsanzo cha zomwe zikuchitika lero ngati n'koyenera.*<br>• Yosefe analangiza Farao kuti akuyenera kusankha anthu amene adzasonkhanitsa chakudya mu zaka za chakudya chambiri ndi kuchisunga kuti anthu adzadye nthawi ya njala. Maganizo amenewa anakondweretsa Farao. Iye anazindikira kuti Mulungu anali ndi Yosefe ndi kuti anali munthu wanzeru. Iye anayika Yosefe kukhala woyang'anira minda yonse ya Aigupto. Mu Aigupto, ndi Farao yekha amene anali wamkulu kuposa Yosefe. ***(Genesis 41:33-45)***<br>• M'zaka za zakudya zambiri, Yosefe anayendayenda m'dziko lonse la Aigupto kusunga chakudya cha zaka za njala. Mu mzinda uliwonse munali nyumba yosungamo chakudya kukonzekera njala imene ankabwera. Pamene njala inafika anthu anali ndi chakudya chokwanira. ***(Genesis 41:46-49)***<br>• *Kumbutsani ana za moyo wa Yosefe mpaka pamene wafika. Kambiranani kuti ichi chinali chikonzero cha Mulungu pa Yosefe kuyambira kale. Mulungu anakhala wokhulupirika kwa Yosefe. Izi zikutanthauza kuti Mulungu sanamusiye yekha Yosefe koma ankachita zinthu molingana cholinga chake pa moyo wa Yosefe. Iye anagwiritsa ntchito nthawi zonse zovuta m'moyo wa Yosefe kuti amuthandize kukonzekera udindo ofunika kwambiri umenewu. Mulungu anagwiritsa ntchito Yosefe kupulumutsa miyoyo yambiri nthawi ya njala!*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br><br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Mtsogoleri watsopano. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika kutero Vesi Yoloweza, ***1 Akorinto 10:13-'Mulungu ndi wokhulupirika'***. Kambiranani tanthauzo la 'kukhulupirika' ndi ana monga tafotokozera. |
| **KUMBUKIRANI** | Funsani ana mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani.<br>• N'chifukwa chiyani Farao anayitanitsa Yosefe?<br>• Kodi chinachitika n'chiyani pa ng'ombe zoyamba m'maloto oyamba aja?<br>• Kodi anathandiza Yosefe kuti amasulire malotowa ndi ndani?<br>• Kodi malotowa ankatanthauza chiyani?<br>• Kodi ntchito yofunika kwambiri ya Yosefe m'zaka za zakudya zambiri inali yotani?<br>• Kodi Mulungu anakhala wokhulupirika motani kwa Yosefe? |

# Malangizo a Aphunzitsi a Kachongedwe ka Maphunziro

**Maphunziro a Kalasi Yoyamba**
- Sabata lililonse pali masamba anayi amene akufunika kuchekenira ndi kulembamo mawu pang'ono.
- Sabata lililonse pali marikisi 20 amene akuyenera kuperekedwa kuchokera pa marikisi 80 a mwezi onse.
- Ana amene akuphunzira maphunziro a Kalasi Yoyamba iwo sakuyenera kuwerenga chifukwa sangathe kuwerenga bwino ndipo tikuyembekezera makolo/owang'anira/atsogoleri awo kuwathandiza.

**Maphunziro a Kalasi Yachiwiri**
- M'buku muli maphunziro anayi pa sabata.
- M'phunziro lililonse muli nkhani. Ophunzira akuyenera kupeza mawu osiyanasiyana m'phunziro, ndi kuchekenira, kutsiriza Mavesi Oloweza ndi zina zambiri.
- Sabata lililonse pali marikisi 20 pa marikisi 80 a mwezi uliwonse pamene atsiriza maphunziro onse molondola.

**FUNDO ZA KACHONGEDWE**

Choyamba aphunzitsi akupemphedwa kuti:
- Onani phunziro lililonse ndipo chongani moyenera zolondola kapena zolakwitsa.
- Perekani marikisi amene mwalangizidwa kutero.
- Nthawi zonse chongani pogwiritsa ntchito mitundu yosiyana ya zolembera, CHONGANI yankho lolondola.
- Lembani yankho lolondola poyenera kutero ndi kukonza mawu olakwika kalembedwe ake, koma MUSACHOTSE marikisi.
- Perekani marikisi ochepa pa yankho lolondola mbali imodzi yokha.
- Phatikizani marikisi onse a pa mwezi ndipo lembani kumapeto pa malo amene mwapatsidwa.

N'kofunika kusaumira ndi kuchita chilichonse chothandiza kulimbikitsa ophunzira kuti aphunzire Baibulo lawo. N'zothandizanso kuti kumapeto kwa mwezi uliwonse mphunzitsi azilemba mawu a chilimbikitso kwa wophunzira pa malo amene aperekedwa. Mutha kulemba ndemanga yoyamikira kuchekenira bwino, zilembo zabwino ndi kumvetsa bwino phunziro ndi zina zambiri.

Yesetsani kuti ndemanga, mafunso, ziganizo, zomwe mwaona ndi zina zambiri zikhale zosiyanasiyana, kuti zithandize kupanga zinthu kukhala zosiyana. Izi zimafunika kuganiza bwino, ndipo ndi kofunika kuti wophunzira azikhala ndi chidwi nthawi zonse. Ngati chiganizo chomwecho kapena funso lomwe likubwera mwezi uliwonse, zimachotsa chidwi cha wophunzira.

**Kalasi Yoyamba**
**Ndemanga zina**
"Chikondi – Ine ndasangalala kuti inu mwayamba maphunziro awa ndipo ndikukhulupirira kuti muwakonda. Zochekenira zanu ndazikonda. Kodi mumapita ku sukulu? Ndikuyembekezera kumva kuchokera kwa inu posachedwa."
"Wachita bwino, Andreya. Wachekenira bwino kwambiri! Kodi zimavuta pamene mumachekenira mizere ya m'kati? Inu musiyako zochepa zokha munachekenira pang'ono phunziro lapita lija."

**Ndemanga zauzimu**
"Wachita bwino, Sarah. Yairo analitu munthu wokondwa kwambiri pamene Yesu anamuthandiza."
"Yankho labwino kwambiri! Nkhani ya kufa kwa Yesu ndi yomvetsa chisoni, koma chokondweretsa ndi chakuti Iye anaukanso."

**Kalasi Yachiwiri**
**Ndemanga zina**
"Yankho labwino, Chimwemwe – Ine ndikukhulupirira kuti aphunzitsi ako akusangalala kwambiri ndi ntchito yako ku sukulu!"
"Ine ndikudziwa kuti posachedwapa ndi tsiku lako lobadwa, Chisomo. Kodi udzachita phwando? Udzachitira kuti? Udzakhale ndi tsiku lopambana kwambiri!"
"Iwe wayesetsa kwambiri. Pali zolakwika zochepa chabe. Usamayiwale kuonanso mayankho nthawi iliyonse."

**Ndemanga zauzimu**
"Ine ndasangalala ndi mmene wachekenira chithunzi cha Yesu ali nkhanda modyera ng'ombe. Kodi sizinali zabwino kuti Mulungu atumize Mwana wake ku dziko lapansi kwa ife?"
"Mitundu yako ndayikonda kwambiri! Zakariya anapereka dipo chifukwa cha kusakhulupirira zimene Mulungu ananena. Iye anakayikiranso Mawu a Mulungu."
"Mayankho abwino kwambiri. Munthu amene anakumana ndi Filipo ku chipululu anapita kwawo akusangalala kwambiri. Iye anamva ndi kukhulupirira nkhani yabwino ya Yesu."

## Zoonjezera A - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B1 | **Moyo Woyambirira** | **Kuyamika m'Nyumba ya Mulungu** |
| | **wa Khristu** | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-simeon-anna/ |
| | | **Kukula mu Nazarete** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-jesus-12/ |
| | | **Kubatizidwa mu Mtsinje wa Yordano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-jesus-baptised/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/mk-john-baptist/ |
| | | **Kuyesedwa m'chipululu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-jesus-tested/ |
| | | |
| B2 | **Zodabwitsa** | **Yesu asandutsa madzi kukhala vinyo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/wedding-cana-preschool/ |
| | | **Yesu achiritsa mnyamata wodwala** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-020-officials-son/ |
| | | **Yesu ndi Bartimeyu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-blind-bartimaeus/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-blind-man/ |
| | | **Yesu achiritsa anthu akhate khumi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-ten-healed/ |

## Zoonjezera A - Kalasi Yachiwiri Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B1 | **Moyo Woyambirira** | **Kuyamika m'Nyumba ya Mulungu** |
| | **wa Khristu** | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-010-simeon-anna/ |
| | | **Kukula mu Nazarete** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-twelve/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-011-jesus-found/ |
| | | **Kubatizidwa mu Mtsinje wa Yordano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/john-baptist-jesus/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-013-jesus-baptism/ |
| | | **Kuyesedwa m'chipululu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-014-jesus-temptation/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-jesus-tempted/ |
| | | |
| B2 | **Zodabwitsa** | **Yesu asandutsa madzi kukhala vinyo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-016-wedding-cana/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-wedding/ |
| | | **Yesu achiritsa mnyamata wodwala** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-020-officials-son/ |
| | | **Yesu ndi Bartimeyu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-blind-man/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/lumo-blindman-jericho/ |
| | | **Yesu achiritsa anthu akhate khumi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-072-ten-leprosy/ |

## Zoonjezera B - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B3 | Betaniya | **Kuphunzitsidwa ndi Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/btbm-mary-martha/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/dm-mary-martha/ |
| | | **Moyo kuchokera kwa Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/btbm-jesus-lazarus/ |
| | | **Kukonda Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/btbm-jesus-anointed/ |
| | | **Kuyang'ana Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-palms-hosanna/ |
| | | |
| B4 | Ambuye Yesu - Mtanda | **Kufa kwa Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-jesus-passover-2/ |
| | | **Yesu amwalira ndi kuyikidwa m'manda** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-jesus-dies/ |
| | | **Yesu akhalanso ndi moyo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-jesus-alive/ |
| | | **Kuchoka kwa Yesu ndi kubweranso kwake** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ndb-ascension/ |

## Zoonjezera B - Kalasi Yachiwiri Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B3 | Betaniya | **Kuphunzitsidwa ndi Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-065-mary-martha/ |
| | | **Moyo kuchokera kwa Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-lazarus/ |
| | | **Kukonda Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-084-jesus-anointed/ |
| | | **Kuyang'ana Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-palms-hosanna/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-078-triumphant-entry/ |
| | | |
| B4 | Ambuye Yesu - Mtanda | **Kufa kwa Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-jesus-passover-2/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ac-barabbas/ |
| | | **Yesu amwalira ndi kuyikidwa m'manda** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-jesus-passover-2/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-099-jesus-burial/ |
| | | **Yesu akhalanso ndi moyo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-jesus-passover-3/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-resurrection/ |
| | | **Kuchoka kwa Yesu ndi kubweranso kwake** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-107-jesus-ascension/ |

## Zoonjezera C - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B5 | Mafanizo | **Msamariya wachifundo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ml-good-samaritan/ |
| | | **Nkhosa yotayika** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rr-lost-sheep/ |
| | | **Mwana wolowerera** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/prodigal-son-preschool/ |
| | | **Wofesa mbewu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/parable-sower-preschool/ |
| | | |
| B6 | Yosefe | **Mnyamata wa maloto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-joseph-dreamer/ |
| | | **M'bale wosakondedwa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-joseph-dreamer/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-joseph/ |
| | | **Kapolo wabwino** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-joseph-prison/ |
| | | **Mtsogoleri watsopano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-joseph-prison/ |

## Zoonjezera C - Kalasi Yachiwiri Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B5 | Mafanizo | **Msamariya wachifundo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rr-good-samaritan/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-064-good-samaritan/ |
| | | **Nkhosa yotayika** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/lost-sheep/ |
| | | **Mwana wolowerera** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-067-prodigal-son/ |
| | | **Wofesa mbewu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-049-parable-sower/ |
| | | |
| B6 | Yosefe | **Mnyamata wa maloto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-joseph-dreams/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/josephs-dreams/ |
| | | **M'bale wosakondedwa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-pit/ |
| | | **Kapolo wabwino** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-joseph-prison/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-prison/ |
| | | **Mtsogoleri watsopano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-pharaoh-dreams/ |

© Bible Educational Services 2023

www.besweb.com

Registered Charity UK CIO 1186004

NY - 03/2024
(Chichewa)